

MAFUNSO NDI MAYANKHO

PA ZISINDIKIZO



[M'bale alankhula mu lirime lina. M'bale wina apereka kumasulira. Osonkhana apemphera mokweza—Mkonzi.]

Atate athu Akumwamba, ife tiri indedi oyamikira chifukwa cha nthawi iyi kuti ife tikhoza kuyanjana kachiwiri pozungulira Mawu a Mulungu, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ife tiri othokoza kuti Inu muli nafe ife, mmawa uno, kuti mutithandize ife ndi kuti mutidalitse ife. Ife tikupempha chikhululukiro cha machimo athu, kuti nyali zathu zikakhoze kudzazidwa ndi Mafuta, ndi zokonzedwa ndipo zikuyaka, kuti Inu mukakhoze kutigwiritsa ife ntchito tsopano kuti tilemekeze Dzina Lanu lalikulu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana wokondedwa wa Mulungu, Yesu Khristu. Amenii.

Mukhoza kukhala pansii.

² Ine ndinali ndikungolowa pamene ine ndinamva uthenga uja ukupita. Kotero ndiri. . . Izo ndi zowona kuti ife tikusowa kusunga nyali zathu zodzaza, kusunga zathu. . . Inu mukudziwa, pomwe. . . Pamene inu muyatsa, inu simungamapitirire pa zomwe inu mumachita, tsopano. Mukuwona? Chifukwa, moto, woyaka mopanda mafuta, umapanga utsi. Kotero ndicho chifukwa chake kukonza kwa. . . kukhala mutakonza nyali zanu, chifukwa utsi pamwamba pa—pa chingwe. Ambiri a inu anthu pafupi usinkhu wanga, pamene ife tinkakonda kugwiritsa ntchito—nyali za mafuta a malasha, mwawona, iwo. . . Iyo—iyo—iyo imakhoza kuchita utsi pamwamba, pamene iyo inali kuyaka, ndipo chotero iwo umasokonezana ndi kuwala. Kotero inu muyenera kupukuta utsi wonse, ndi kuti ife tikhoza “kulimbika cha mtsogolo, molunjika ku malo a kuyitana kwa pamwamba mwa Khristu.”

³ Tsopano, uli—uli waukulu, mmawa wokongola, kunja ndi mkati, pamene nyengo ya Chiwukitsiro iyi ikuyandikira tsopano.

⁴ Ndipo—ndipo ife tiri tsopano kubwera ku Chisindikizo chotsiriza, usiku uno, Ambuye akalola. Ndipo Ndicho Chisindikizo chachinsinsi kwambiri, kwambiri, kwambiri, chifukwa Icho sichiri ngakhale—Icho sichiri ngakhale kutchulidwa mu Malemba paliponse, popanda zophiphiritsa, chirichonse choti nkugwirapo. Icho chiyenera kubwera molunjika kumene kuchokera Kumwamba.

⁵ Ndipo ilo—liri—kukhala ngati ora lomangika kwa ine. Ilo lakhala liri, sabata yonse. Tsopano ili liri langa. . . likhala

tsiku lachisanu ndi chitatu langa mu chipinda. Ndipo ine ndinazindikira mkati muno, ambiri, mu zopempha izi, ine ndinakhala ngati kusankhapo. Analipo ambiri a iwo amene amafuna zolankhulana padera. Ndipo ine—ine ndimakonda zimenezo. Ndikanafuna kuti—kupereka izo tsopano, mwawona, koma ine—ine sindingakhoze pakali pano. Chifukwa, inu mukumvetsa, kuti z—zonse za zomwe ife tikuyesera kuchita tsopano ziri kupeza vumbulutso la chifuniro cha Ambuye, inu mukuwona. Ndiye ife kuti tikhale ndi kulankhulana padera, ndiye izo zimakukokera iwe kumbali, kupita kumbali yina ya chinachake, mwawona.

⁶ Ndipo, ndiye, ndipo monga mu pemphero kwa odwala, ndicho chonse palimodzi chosiyana. Iwe... Ali masomphenya ndi zinthu; iwe umawerenga mosiyana, ndipo iwe—iwe umadzedwa mosiyana. Ziri monga momwe Baibulo linanena apo, “M—mtengo umene wabzalidwa mphepete mwa m—mitsinje ya madzi.” “Mitsinje ya madzi,” mwawona, madzi omwewo, koma pali wotulutsa umabwera njira *iyi*, njira *iyi*, ndi njira *iyi*. Zidalira pa wotulutsa wuti. Ndi Mzimu womwewo.

⁷ Paulo, Akorinto Woyamba 12, anachita chinthu chomwecho, analankhula za, “Pali mphatso zambiri, koma ndi Mzimu womwewo.”

⁸ Koteru, inu mukuwona, ngati inu mukugwira ntchito, monga, ndi chinthu chimodzi, ndiye nkusinthidwa kubwera ku chinthu china ichi cha *apa*. Inu mukudziwa chomwe ine ndikutanthawuza. Iwe—iwe umawerenga kutsata mzere umenewo, iwe wawatenga anthu... Ndipo tsopano mitima yawo yonse yakhazikika, “Zisindikizo izi ziri chiyani?” Chidwi chawo, “Nchiyani Icho?” Usiku ndi usiku, pamene ine ndibwera muno, mumakhala kumangika koteru, mpaka ine ndiyenera kulankhula za chinachake; kukhala ngati kutenga—kuchitontholeta icho, inu mukuwona, ndipo, ndiye, mpaka Mzimu Woyera utamatula Chisindikizo. Ndiyeno—ndiye ine ndiyenera kutero, usiku uliwonse monga choncho. Ndiye pamene ife tisinthira izo ku machiritso kapena chinachake, mwawona, iwe... Anthu onse akhazikika pa chinthu chimodzi. Iwe sungasinthe nkomwe icho kubwerera ku china, pomwepo.

⁹ Ndipo—ndiyeno, aponso, podziwa kuti pakati panu pomwe zinthu zikuchitika, mwawona, zomwe ine—ine ndiri chabe... ine—ine ndikudziwa. Ine ndikudziwa inu—inu simukuziwona izo, mwawona. Ine ndiri wotsimikiza basi kuti inu simukuziwona izo, mwawona. Ndipo inu mukuti, “M’bale Branham, ndicho chinthu cholimba kuti inu munene icho.” Ine ndikudziwa kuti chiri.

¹⁰ Koma, penyani, mungondirola ine ndingonena izi tsopano. Ine ndikuganiza awa ali chabe matepi a ifeeni, ndi zina zotero. Koma mundirole ine ndinene izo, mwawona. Kutu,

inu—inu simuku. . . Inu simukumvetsa izo, mwawona, ndipo inu simukuyenera kuzimvetsa izo. Kotero musayesere kutanthawuzira chirichonse, mwawona. Musati muyesere kuyika kutanthawuzira kwanu kwa izo; inu kokha—inu mungopita nazo kutali. Ingotangani langizo langa, ngati inu mukundikhulupirira ine tsopano, ngati Mulungu ali—wandipatsa ine mwayi pamaso panu.

¹¹ Ndipo inu mukudziwa, kuti, mavumbulutso awo ndi zinthu. Ine—ine ndakhala pano ndi inu nthawi yayitali, mwawona, ndipo izo nthawi zonse zakhala zolondola. Ndipo tsopano kutsimikizira pawiri izo, kulondola, zimagwirizana nawo kumene Mawu. Mukuwona? Kotero, inu mukudziwa Ziri PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndizo chimodzimodzi. Mwawona, Izo zatsimikiziridwa kwa inu.

¹² Tsopano tengani langizo langa, monga m'bale wanu. Musati muyike kutanthawuzira kwanu kwa chirichonse. Inu musingopitirira ndi kukakhala moyo wabwino wa Chikristu. Chifukwa, inu mudzangozipota kokha nokha kuchoka kwa chinthu chenicheni pamene inu muchita izo. Mukuwona? Inu, inu mudzangopota kokha njira yanu kachiwiri kuchoka ku chinthucho.

¹³ Ndipo nonse a inu muli ndi chikumbumtima ndipo mukudziwa kuti pali chinachake chachinsinsi chikuchitika. Ndipo icho chikuchitika. Ndipo ine ndikudziwa chomwe icho chiri. Tsopano, sindikungonena chabe izo; icho ndi chisomo cha Mulungu chomwe chikundirola ine kudziwa chomwe icho chiri. Ndi chinachake chomwe chiri chopambana. Ndipo icho chapita pakali pano, ndipo palibe njira mu dziko yoti inu muchiwonere icho. Ndipo chiri. . . ine. . . Koma, kotero ndithandizeni ine, ndi Baibulo ili mu dzanja langa, ine ndikudziwa chomwe icho chiri. Icho chakhala chikuwuzidwa kwa inu, kale. Kotero basi—basi musati muyesere kuyika kutanthawuzira kulikonse, koma ingondikhulupirirani ine, monga m'bale wanu. Mukuwona? Ife tiri kukhala mu ora lalikulu. Ife tiri kukhala mu nthawi kumene. . . Chabwino, tiri. . .

¹⁴ Tsopano, inu ingokhalani odzichepetsa kwenikweni, khalani Mkhristu, ndi kuyesa kukhalira moyo Mulungu. Ndi kukhala moyo wowona mtima naye munthu mzanu, ndipo muziwakonda iwo omwe sakukondani inu. Musati muyesere kupanga chirichonse. . . Inu mukuwona, inu mukatero, inu mungochipanga icho chachinsinsi chinachake, ndi kusokoneza dongosolo lenileni la Mulungu. Mwawona?

¹⁵ Dzulo madzulo, chinachake chinachitika mu chipinda changa, chomwe ndidza—sindidzakhoza konse ku—kuchisiya icho, inu mukuwona. Ndipo kotero inu. . . Ndipo pafupi masabata awiri apitawo, chinachake chinachitika, icho sichidzakhoza konse. . . Malingana ngati ine ndikhala pa

dziko lapansi ili, ine—sindidzakhoza konse kuchoka kwa icho, mwawona. Ndipo, kotero, koma . . .

16 Ndipo m—mpingo, inu simukuyenera kudziwa zinthu izi, kotero musati muyike kutanthawuzira kwa chirichonse. Mukuwona? Inu muzingopitirira ndipo muzingokumbukira zomwe mwawuzidwa. Mukakhale moyo wa Chikhristu. Muzipita ku mpingo wanu. Khalani nyali yeniyeni paliponse pamene inu muli, ndipo muzingotenthera Khristu, ndi kuwawuza anthu momwe inu mumamukondera Iye. Ndipo mukangolola umboni wanu ukakhale nacho chikondi, nthawi zonse, ndi anthu. Mukuwona? Chifukwa, ngati inu simutero, inu mukuzipotera nokha mu chinachake kumeneko, ndiyeno muli—mwachoka pa njira yopunthidwa. Mwawona, nthawi iliyonse mukuyesera kuchita icho, inu mwachita zimenezo. Mukuwona? Kotero basi musati, musati, musati muyesere kupanga kutanthawuzira ayi.

17 Ndipo makamaka, usiku uno, pamene Chisindikizo icho chikubwera patsogolo pa inu, mwawona, basi musati muyesere kuchitanthawuzira Icho. Inu muzingopitirira patsogolo ndi kukhala odzichepetsa basi, ndi kumapitirira nawobe Uthenga womveka womwewo.

18 Tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo . . .Ife, pokhala Mpingo wa Mulungu wamoyo, tisati ife . . .” Chabwino, monga ine ndimayesera . . .Penyani apa, ine ndikufuna kunena . . .Kunena, “Chabwino, ine ndilekerenji? Ine ndiyenera kukhala . . .” Ayi. Tsopano, musatero.

19 Kumbukirani, ine ndikunena izi kwa ubwino wanu. Mwawona, ine ndikunena izi kotero kuti inu mudzamvetse. Ngati inu mumandikhulupirira ine, tsopano, mverani kwa zomwe ine ndikuwuzani inu. Mukuwona? Mukuwona?

20 Tsopano, apa, tsopano apa pali chipirala, ndipo, ndicho, ife tichitcha icho chipirirara chomverera, mwawona. Ndipo mwa icho, muli wailesi, mwawona, ndipo umu muli machenjezo ndi zinthu zomwe zingakhoze kuchitidwa. Monga lupanga mu dzanja lanu, mwawona, iyo ikhoza kugwira kuchokera kwa choyipa kapena kuchokera kokha pamene yake . . .iyo igwira uthenga wake, mwawona.

21 Tsopano, koma tsopano, mwa chitsanzo, kwa munthu wamba, pakhala pali miyambo yochuluka ndi mafuko zikuwuka, pa kutsanulira kwakung’ono kwa Mzimu, mpaka anthu akufika onse podzichititsa mu mulu wa zinthu, kutuluka ndi kukayamba mayendetsedwe ena aang’ono, ndipo, inu mukudziwa, ndi chinthu. Mukuwona? Inu simukufuna kuchita izo tsopano. Mukuwona? Tsopano, ingokumbukirani, ingokhalani mwanjira yomwe inu muli.

22 Ndipo inu mukuti, “Chabwino, Ambuye andiwonetsa . . .” Ayi. Tsopano ingokhalani osamala, mwawona.

23 Penyani apa. Mundirole ine ndikuwonetseni inu chinachake, mwawona. Kodi inu mumadziwa kuti muli zikwi khumi za maliwu mu chipinda chino pakali pano? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kwenikweni, maliwu a anthu omwe akubwera kupyola mu mphepo za magetsi za walesi! Bwanji inu simukuwamva iwo? Iwo ndi maliwu. Nkulondola uko? [“Ameni.”] Iwo akuyandama kupyola momwe muno tsopano. Pali mawonekedwe a anthu ndi matupi akuyendayenda kupyola mu chipinda chino tsopano. Nkulondola uko? [“Ameni.”] Chabwino, bwanji inu simukuwawona iwo? Mukuwona? Iwo ali muno, maliwu enieni monga liwu langa. Chabwino, bwanji inu simukuwamva iwo? Mukuwona? Iwo ayenera kukhudza chinachake poyamba, kuti chiwulule iwo. Mukuwona? Tsopano inu mukumvetsa? [“Ameni.”]

24 Tsopano basi musati mutanthawuzire kanthu. Ngati Mulungu akufuna inu mudziwe chirichonse, Iye adzatumiza icho kwa inu. Mukuwona? Kotero ingokhalani enieni, olimba kwenikweni tsopano. Gwiritsanibe, chinachake chachitika. Ndipo tsopano ingokhalani kwenikweni. . . Inu mukumvetsa zomwe ine ndikutanthawuza, sichoncho inu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo ingokhalani. . . Musati muyesere kudzipanga nokha achirendo, kuti mukhale Mkristu, chifukwa inu—inu mumadzichotsa nokha nkutalikira ndi Mulungu. Ndipo inu—inu—inu. . .

25 Ngati inu mungakhoze kumvetsa izo, ichi ndi Chikoka Chachitatu chija. Mukuwona? Inu—inu mukanayenera kuchigwira icho, tsiku lina. Mukuwona? Kotero ndiye, ingokumbukirani, apo sipadzakhala zowonera monga zinalipo za zina ziwiri. Mukuwona? Kotero, ndizo mpaka momwe inu—inu muyenera kudziwa tsopano. Basi—ingokumbukirani icho. . .

26 Inu mukuwona, tsopano, pali chinachake chikuchitika mu chipinda chino, ndipo pali Chinachake pano. Apo pali—apo pali, weniweni, mu chipinda chino, Angelo, Liwu la Mulungu. Mukuwona? Koma inu muchita motani. . . Inu simungakhoze. . . Ngati inu simungakhoze kumva liwu lachibadwa, lopanda chinachake cholitumiza ilo, inu mumva bwanji Liwu lauzimu?

27 Tsopano inu mukhoza kukhulupirira-modzipangitsa kuti winawake akuyimba nyimbo yinayake *iyi*. Iwo akhoza ngakhale kusakhala alipo, mwawona. Koma pamene ilo ligunda kwenikweni krustalo yomwe ilo likuyenera kugunda, ndiye ilo limapereka kutanthawuzira kuwona, ndi kuwonetsa, kutsimikizira ilo mwa kusonyeza chithunzi. Mwawona chimene ine ndikutanthawuza? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

28 Tsopano, Mzimu wa Mulungu, pamene Iwo ulankhula kupyolera mu Mawu owona, Iwo umadzitsimikizira Wokha, kuti udziwonetse Wokha, kuti Uli kulondola. Inu mukumvetsa tsopano? [Osonkhana “Ameni.”—Mkonzi.]

Tsopano tiyeni tipemphere, basi kachiwiri.

²⁹ Atate Akumwamba, ife tiri pafupi kuti ti-. . .kutsegula zivindikiro za Bukhu ili, ndipo monga gawo la thupi la—la kuyesera kuperekanso ku zomwe Inu mwatsegula kwa ife mu malo auzimu. Ndipo tsopano ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudzandithandize ine kupereka kutanthawuzira kolondola ku mafunso awa. Kuti zikakhoze kunenedwa kuti—kuti iwo ali. . .Iwo ali woti athandize anthu. Iwo ali woti awapatse iwo kumvetsa. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mudzapereke kwa inu kumvetsa, kuti ine ndikakhoze kuwatumiza Iwo kwa anthu Anu, kuti iwo akakhoze kukhala nako kumvetsa, kuti palimodzi ife tikakhoze kukhala moyo kwa ulemero ndi ulemu wa Mulungu, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰ Tsopano, ine ndimangofuna kunena izo.

³¹ Ndipo ine ndimaganiza chinthu ichi *apa* chimawongolera matepi awo, koma icho sichikutero, mwawona. Ndipo ili ndi—getsi la pa tebulo. Ndipo ine ndimaganiza chowongolera tepi chinkakhala apa. Koma ine ndinawuzidwa kuti ndizingosonyeza kwa abale mu—mu chipinda uko, chipinda chojambulira, ndipo iwo azidziwa poti ayimitse matepiwo, ndipo poti asatero.

³² Mwawona, matepi ali ndi utumiki wa mdzikoponseponse kulikonse, mwawona, kulikonse. Iwo amapita mu zilankhulo za mtundu uliwonse ndi chirichonse. Kotero pali zinthu zomwe ife tikananena pomwe apa, zomwe ife sitikananena kwinakwake, inu mukuwona, ndipo ndicho chifukwa chake iye timayimitsa iyo.

³³ Tsopano, kuyankha mafunso ndi chinthu ndithu. Kotero, ine—ine tsopano. . .Mu—mu—mu kuyankha kwa izi, ambiri a iwo, ambiri a mafunso, kunja kwa. . .Tsopano, limodzi lililonse. . .Ena a iwo sakukhudzana nkomwe ku Uthenga, nkomwe, koma ine ndichita. . .kapena Zisindikizo nkomwe, koma ine ndiyesa kuwayankha iwo. Ndipo iwo anapatsidwa kwa ine, ndipo monga iwo anawuzidwa. Ine ndinawuzidwa kuti ambiri a iwo. Kapena, gawo lalikulu la iwo anali a mapempho a pemphero, ndipo odwala ndi osawutsika. Ndi—ndi zinthu zosiyana monga choncho, izo zikupitirira, ndipo kotero izo zizinakhudze chirichonse kwa funso lililonse loti liyankhidwe. Ndiyeno iwo. . .Ine ndinapatsidwa mulu womwe unali—omwe anali a zinthu zosiyana, Lemba ndi zinthu; koma mwinamwake, ngati ife tiri nayo nthawi, ife tidzayesa kuwayankha iwo mwakukhoza momwe ife tingathere. Tsopano, ndipo ngati ine ndilakwitsa, bwanji, kumbukirani, izo sitinalinge kulakwitsidwa.

³⁴ Kotero kodi aliyense akumverera bwino? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Amen. Siziri izi choncho. . .Kukamba za malo Ammwamba mwa Khristu Yesu, ndi malo odabwitsa bwanji, ndi nthawi yodabwitsa bwanji!

35 Za nthawi yonse yomwe ine ndakhala kuseri kwa guwa ku kachisi, ine sindinati nkomwe, nkomwe, mu nthawi iliyonse ya utumiki wanga, kugwirapo ntchito konse mu madera a Mulungu ndi madera a mzimu monga zinaliri nthawi iyi; kuposa chirichonse chomwe ine ndinachitapo mu nthawi iliyonse ya utumiki wanga, mu msonkhano uliwonse kulikonse, monga uwu. Kwambiri, zakhala pa machiritso. Uku ndiko kuwulula kwa Zowonadi, mwa Mzimu womwewo, Mzimu womwewo.

36 Ndipo ine—ine ndakhala kwa ndekha, pamodzi, ndipo ndinali ndikukhala ku malo, kapena kupita uko kukadya ku malo. Ndipo ine ndangokhala ndiri ndekha, kotero iyo yakhala ili kwenikweni nthawi yopambana.

37 Ndipo tsopano, mosachedwetsa, kapena mmawa uno, kapena mmawa wotsatira, ine...Mwinamwake, ngati ife tingakhoze kutsiriza mu nthawi, ine ndidzangopempherera odwala mmawa uno, ngati mafunso awa satha motalika.

38 Kotero ine—ine ndiyenera kukakhala kwa ndekha kanthawi pang'ono, mwawona. Malingaliro a munthu akhoza kokha kupirira mochuluka chotero. Mukuwona? Ndipo pamene iwe ufika pa malo pamene iwe ukukhala pansi ora, utachititsidwa zanzi nako Kukhalapo kwa Mulungu, ndi Lawi la Moto litapachikika pamenepo pamaso pa iwe, iwe—iwe sungapirire icho motalika kwambiri, inu mukuwona. Munthu sangakhoze, sangakhoze kupirira izo.

39 Ndipo kotero, tsopano, mafunso awa ali kwenikweni abwino. Ine ndikuyamikira, ndi nzeru ndi zinthu zomwe anthu akugwiritsa. Tsopano, kwa limodzi loyamba. Ndipo ine ndiyesa kuwayankha iwo. Ndiyeno ngati ine—ine sindilitenga ilo molondola, chabwino, inu—ine ndiye mundikhululukira ine.

40 Ndipo ngati inu muli nako kutanthawuzira kosiyana, ndipo mu kukhulupirira kuti lingaliro lanu pa ilo liri lolondola, chabwino, ingomapitirirani patsogolo choncho. Icho sichipweteka, chifukwa palibe pafupi limodzi kapena awiri a iwo omwe akukhudzana ndi chirichonse ku chipulumutso. Ali kokha...

41 Ambiri a mafunso ali, afunsidwa, pa mbali iyi ya chits-... kapena pa Mkwatulo wa Mpingo. Kotero, mwawona, ndi mafunso cha apa, zomwe ziri zoti zibwera ndi zomwe ziti zidzachitike, cha ku mbali zina. Chifukwa, ife tsopano tapyola m'badwo wa mpingo, mu zophunzitsa zathu mu—mu Bukhu. Ife tapyola, mpaka mu nthawi ya kuyitana zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi. Tsopano limodzi loyamba apa:

173. Kodi anamwali asanu ochenjera, a Mateyu 25, ali otumikira kwa—kwa Mkwatibwi, kapena ali iwo Mkwatibwi? Mukuwona? Ngati anamwali ochenjera awa ali otumikira kwa Mkwatibwi, nanga Mkwatibwi ali kuti?

42 Mwawona, tsopano, mwa kukhoza kwa kumvetsa kwanga, anamwali asanu awa . . . Analipo khumi a iwo, inu mukudziwa, amene anatuluka, mwawona. Ndipo izi apa zangokhala chophiphiritsa, kapena fanizo, mwawona, zomwe—zomwe ine nditi ndikuwuzeni inu. Mwawona, analipo khumi a iwo. Chifukwa, apo analipo oposa khumi. Iyo inangopangidwa nambala. Koma, ndiye, a—anamwali ochenjera anali nawo Mafuta mu nyali zawo. Opusa analibe Mafuta mu nyali zawo.

43 “Kotero ngati khumi awo uko, a Mateyu . . .” Ili liri—funso la munthu. “Ngati khumi awo, apo, kodi izo zinkatanthawuza kuti awo akanadzakhala . . . kapena asanu awa, kani, kuti akanadzakhala asanu chabe, mwawona, anthu asanu chabe?” Ayi, izo sizikutanthawuza zimenezo.

44 Ichō chiri chabe chophiphiritsa, cha anamwali, inu mukuwona, cha namwali yemwe anatuluka ndi Mafuta mu nyali zawo. Iwo ali gawo la Mkwatibwi ameneyo. Ndipo mwakumvetsa kwanga . . .

45 Ndiyeno inu muzindikira, tsopano, kuti iwo anali anamwali a ulonda wotsiriza. Akubwera mmusi kupyola mu mawulonda, apo panali mawulonda asanu ndi awiri. Ndipo mu ulonda wachisanu ndi chiwiri, ora la pakati pa usiku, monga ife tikugundapo tsopano, mwawona. Tsopano, mu ulonda wapakati pa usiku uwu, anamwali awa anawuka ndipo anapukuta nyali zawo, ndipo anakalowa mkati; pamene anamwali ogona . . .

46 “Tsopano gawo ili apa, asanu awa,” ngati ndilo tanthawuzo la funso, likutanthawuza chiyani, “kodi analipo asanu okha?” Ndipo ife tiri nawo mafunso ambiri apa, a z—zikwi zisanu ndi ziwiri, ndi ena otero. Tsopano, icho, icho chinali chabe chophiphiritsa, gawo la iwo. Ndipo onse amene anawuka mu m’badwo wotsiriza uno apa, ulonda wachisanu ndi chiwiri, omwe . . . “Ngati apo panalibe koma—koma asanu omwe anawuka pa nthawi imeneyo, omwe anasinthidwa, nalowa mkati ndi Mkwatibwi, zina zotero, Mkwati? Tsopano ngati iwo eniake . . .”

47 Izo sizikutanthawuza kuti pakakhala asanu okha. Chifukwa, iwo ali anamwali ogona, monse mmusi kupyola mu mibadwo; monga ife tabwerera sabata iyi, mwawona.

48 Mu masiku a—a Paulo, mngelo wa mpingo ku Efeso; Paulo, kuyambitsa mpingo uwu, pokhala mtumiki kwa iwo. Kumbukirani, Paulo, poyambitsa mpingo ku Efeso, anakhala mtumiki kwa mpingo umenewo. Ndipo Mzimu, unali mu dziko nthawi imeneyo, unali Mzimu wa mkango. Ndipo mkango uli Mkango wa fuko la Yuda, yemwe ali Khristu, ndipo Khristu ali Mawu. Paulo, ndi Mawu a m’badwo umenewo! Zikwi zinagona mu m’badwo umenewo. Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

49 Ndiye panabwera m'badwo wotsatira, ndipo pa nthawi yomwe mpingo unakhazikika mu—mu m'badwo wa mdima, Mzimu wa wa ng'ombe unatuluka; ntchito, kuvutikira, ndi nsembe, ndi kupereka miyoyo yawo. Zikwi kuphatikiza zikwi zinagona, pansi pa kufera ndi chirichonse. Iwo akuyembekezera, mwawona.

50 Ndiye, ndipo m'badwo wotsatira unabwera, Achilutera, m'badwo wa kukonzanso. Apo panapita wanzeru kwambiri, mu kukanika kwa munthu. Ngati inu mungazindikire, munthu anatulukira ndi izo, ndipo, pamene iye anatero, iye anawonjezera kuthyathyalika kwakekwake. Ndicho chimene chinamukwatiritsa iye ku mbali yina, mwawona. Mukuwona? Ngati iye akadangokhala ndi nzeru za Mulungu, kumangokonzanso ndi kukokera kunj... Koma kodi iye anachita chiyani? Atachoka munthu uyo yemwe anali nawo uthenga, Lutera; itachitika imfa ya Lutera, iwo anali nalo bungwe la Chilutera.

51 Itachitika imfa ya Wesile, iwo anali nalo bungwe la Amethodisti. Mukuwona? Apo, inu muzingopitirira mwanjira imeneyo. Izo—izo basi... Izo zimachita zimenezo. Tsopano ine ndikufuna inu ku—ku—kuti muzindikire ichi, mwawona. Tsopano winawake akhoza kufunsa za Chipentekoste, umene unali—m'badwo wachitatu.

52 Inu mukuwona, umodzi uliwonse wa mibadwo imeneyo unkadziviika kokha mu Mzimu Woyera. Kulungamitsidwa ili ntchito ya Mzimu Woyera; kuyeretsedwa ili ntchito ya Mzimu Woyera; koma ubatizo *uli* Mzimu Woyera. Ndicho chifukwa chake chinatengera Mneneri wauneneri kuti abwere pansi. Osati mtumiki ku m'badwo, chifukwa Mzimu Woyera unabwera Mwiniwake, mu chidzalo Chake, cha ubatizo.

53 Koma pa mapeto a m'badwo, monga nthawizonse zimathera pa yina, ife tikupeza pamenepo, ndiye, mtumiki akutumizidwa. Ndipo zophwasuka zonse izi ndi zinthu nzoti ziyikidwa mu malo ake monga choncho, ndiye Mkwatulo ubwera kwa Mpingo.

54 Koma onse omwe akuyika zinthu zonse zosiyana izi, “Dzuwa likusandulika kukhala mdima, mwezi...” Iwo amaziyika mwanjira iyo apa mu m'badwo wa Chikhristu. Iwo amangolephera kuwawona mafunso atatu awo omwe anafunsidwa Ambuye wathu pamenepo, mwawona, pamene Iye anawayankha iwo.

55 Tsopano, usiku watha, ine ndikuganiza palibe funso nkomwe. Ife tinatenga limodzi lililonse la mafunso amenewo ndi kuwayika iwo pansi pomwe pa Zisindikizo. Ndipo Zisindikizo ziri Bukhu lonse pamodzi, llolokha.

Inu mukukhulupirira zimenezo, adokotala? [M'bale ati, “Inde.”—Mkonzi.]

⁵⁶ Mwawona, chinthu chonse changokutidwa pamodzi. Ndipo ife tinatenga zomwe Yesu ananena apa. Iwo anafunsa mafunso atatu, mwawona, “Zidzakhala liti zinthu izi? Chidzakhala chiyani chizindikiro cha Kudza Kwanu? Ndipo ndi chiyani mapeto a dziko?” Ndipo Iye anabwera mmusi kumene. . . Ndipo ife tinawasolola iwo, limodzi lirilonse, pansi pa izo, koma chimodzi. Chinali chiyani icho? Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri. Chifukwa? Mwawona, icho sichikudziwika. Ndicho icho. Chimodzi chirichonse cha izo zinatuluka bwino. Ine ndinazifanizitsa izo, chimodzimodzi ndithu, mmbuyo ndi mtsogolo.

⁵⁷ Ndipo, ine, pamene ine ndinalembe usiku watha, ndipo ine ndinafika mmenemo ndi kufika ku. . . Ine ndinapita mmbuyo kukayang’ana pa cholembe changa cha kale ine ndinatenga kuchokera—kuchokera kumbuyo uko. Chabwino, ine ndinawona pamene ine ndinayika chimodzi mu malo ena, monga choncho. Ine ndinasemphanitsa izo, mmbuyo ndi patsogolo. Ndicho chimene ine ndinachita. Ine ndikuganiza inu munachigwira icho. Inu, inu munachigwira icho? Mukuwona?

⁵⁸ Ine ndinali nditalembe pansi apa zomwe ine ndimati ndilembe pa *izi* mbali yina, ndipo ndinalembe izo cha *apa*. Kuyika—kuyika zonse za izo, 9, 11, kapena 9, 6, kapena chiyani. . . kapena 6 ndi 11, ndi—ndi—ndi 9 ndi 11, chomwe sizinali chomwecho. Chinali mosemphanitsa, ndime yotsatira pansi pa iyo. Mukuwona? Ndipo ilo linali ilo, y—yankho, pakati pa chowawitsa ndi nkondo, inu mukuwona. Ndipo pamene izo zinali.

⁵⁹ Kotero ine ndinangokhala wokondwa! Ine ndinali kumangopitirirabe monga—a. . . Ine ndinali kusangalala nako kukondoweza kochokera mu vumbulutso. Kotero, ine—ine ndinayika izo, ichi cha apa. Nditakhala pamenepo ndi pensulo, kapena peni, ine ndinalembe 11 pa malo onsewo, pamene izo sizimayenera kukhala. Ine ndikuganiza inali 9 mmalo mwa 11 ku mbali yinayo.

⁶⁰ Koma tsopano kodi inu munawona momwe izo mwangwiro zinagwirizirana? Tsopano, musati muyiwale zimenezo. Izo zikugwirizana kutsika mpaka ku Chachisanu ndi chimodzi, ndipo zinayima, mwawona. Ndipo yang’anani—yang’anani kutsegula kwa Zisindikizo; izo zikubwera mpaka ku Chachisanu ndi chimodzi, ndi kuyima. Basi, “Kachetechete Mmwamba,” ndicho chonse icho chinanena, “kwa danga la theka la ora.”

⁶¹ Tsopano—tsopano, mu izi, mwawona, ine. . . ine ndisowa kufulumira ndi kuyankha awa. Chifukwa, mwawona, limodzi lirilonse la iwo liri ulaliki, wotalika masabata anayi, inu mukuwona, pa—pa limodzi lirilonse, ndipo inu iwe ungochoka pa chinachake. Koma ine—ine sindikutanthawuza kuchita izo, chifukwa ine ndikufuna kutenga funso la aliyense, mpaka momwe ine ndingathere.

62 Anamwali awa, mwawona, iwo anapangidwa mwa . . . Ndilo chabe gawo la iwo, mu m’badwo umenewo, mwawona. M’badwo uliwonse uli nawo anamwali. Mukuwona? C—Chisindikizo . . .

Mngelo akubwera kwa mpingo. “Kwa mngelo wa mpingo wa Efeso lemba.” Mukuwona?

63 Ndiye kufika cha apa, ndiye zitatha zolemba ku mpingo wa Aefeso, fanizirani izo mmbuyo, Chisindikizo chatsegulidwa. Ndimo chabe momwe ife tikubweretsera izo, kuyesera kubweretsa izo zonse kwa inu, (mwawona chomwe ine ndikutanthawuza?), ngati Ambuye alola.

64 Poyamba iwo amakhala ndi chiyani? Mibadwo ya mpingo. Nkulondola uko? Chinthu chotsatira, uthenga kwa mibadwo ya mpingo. Aliyense akumvetisa momveka izo tsopano? Mukuwona?

65 Poyamba, ife tiri ndi mibadwo ya mpingo, ndipo tiri ndi mbiriyakale, kuyala pansu mabungwe a Nicaea ndi mabungwe a pre-Nicaea, ndi chirichonse chomwe ife tikanakhoza kupeza mu mbiriyakale, ndipo tinapeza kuti kumasulira kolondola kwa Mawu kunali chimodzimodzi ndi mbiriyakale. Ndi kuzibweretsa izo mmusi ku tsiku lino, mu Laodikaya uyu. Ndipo inu—inu simukusowa kukhala ndi mbiriyakale ya iwo; uku kuli kupanga mbiriyakale tsopano, mwawona. Apo iyo ili. Ndipo, ndiye, tinasonyeza zomwe ziti zidzakhale mu m’badwo uno.

66 Tsopano ife tabwerera ndi Zisindikizo, ndi kutsegula Chisindikizo chimenecho. Mulungu akutsegula Chisindikizo icho kwa ife. Nchiyani icho? Poyamba, pali mtumiki, m’badwo wa mpingo; potsatira pali Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri.

67 Tsopano, ife tikupeza chivundi chomwe chikugunda m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri. Koma Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri sichikuwulula chirichonse, chomwe chiti chikachitike kwa icho. Mukuwona? Chifukwa, pa mapeto a m’badwo wa mpingo umenewo ndi poti pabwere mphatso ya uneneri kuti uwulule zinthu izi. Mukuwona? Kodi inu mukutsatira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. Tsopano zindikirani momwe chimodzi chirichonse cha Zisindikizo zimenezo . . .

68 Ndiye ine ndikubwera cha apa, ndipo mafunso atatu awo anafunsiwa Yesu Khristu, “Chiyani, zidzakhala liti zinthu zimenezi, ‘Pamene sipadzakhala mwala umodzi pa umzake?’ Ndi liti pamene uyu adzagwetsedwe pansu, chirikati ichi cha zachipembedzo za mu dziko, ndipo china kuyikidwapo? Mwawona, izo zidzakhala liti?” Kukwera kwa wotsutsakhristu! Mukuwona? Ndipo nchiyani chinatuluka kukakomana nacho icho? Mawu, Mawu kutsutsana ndi mawu.

69 Ndiye izo zinakhazikitsidwira ku ndale ndi china chirichonse, ndipo apo panapita ntchito ya ng’ombe. Mukuwona? Ndizo chimodzimodzi chachiwiri apa. Ndipo Yesu ananena choncho, mu Mateyu 24, mwawona. Ndiye ife

tikubwera mmusi kuchokera kwa icho, ku kukanika kwa okonzanso, Chamoyo cha munthu chinatuluka kukakomana nacho icho. Ndizo zomwe zinachitika. Ndiye ife tikubwera mmusi, chotsatira, ku Chisindikizo Chachinai, pamene wotsutsakhristu akukhala zosakanizika, ndipo anali nalo dzina, “Imfa.”

⁷⁰ Tsopano yang’anani zomwe Yesu ananena, “Ndipo iye akanakhoza kumuponyera iye ku moto, ndipo ngakhale kupha ana ake.” Ndiyo imfa, kukwera. Ndiwo onse Aprotestanti ndi Akatolika, chizindikiro cha imfa pa mmodzi aliyense wa iwo. Mwawona, “Iye ndi ana ake awonongedwe.” Kotero ngati inu mukudalira pa chipembedzo chanu, kulibwino inu muchoke kwa icho pakali pano.

⁷¹ Ndiyeno pamene zikufika kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, Yesu anayimira pomwe apo. Iye anatsogola Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, pa kunena, “Mwezi udzasandulika magazi, ndi mdima ndi chirichonse.” Zinthu izi zikanadzachitika. Ife tikubwera cha pomwe apa ndi kutsegula Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi. Chitatha kutsegulidwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, ndiye nkupotokera mmbuyo momwe ndi kuwonetsa chinthu chomwecho.

⁷² Ndi zimenezotu, ndi malo atatu osiyana mu Lemba, tinawamangiriza iwo pamodzi ndi vumbulutso. Mukuwona? Yang’anani. Malo amene Yesu ananena choncho; malo omwe pamene Iye anatsogola Bukhu, izo zinabisika kuchokera ku maziko a dziko; ndiyeno vumbulutso la tsiku lino apa, kuziyika izo momwemo umo, kumangiriza zitatu palimodzi. Ndipo katatu uli umboni. Kotero, izo nzowona. Izo nzowona mwamtheradi.

⁷³ Tsopano, anamwali awa amene akubwera motsatira apa, iwo ali amodzi omwe anagona, ndiyeno thupi lonse lapangidwa pamodzi nalo gulu limenelo. Lomwe likupita kukapanga...mwawona, kukapanga a—anamwali ochenjera. Ndipo anamwali opusa ali amodzi omwe anayamba kumbuyo uko pa nthawi yomweyo yomwe anamwali ochenjera anayamba, wotsutsakhristu, ndipo iwo ali amodzi omwe akuyesa kugula Mafuta.

⁷⁴ Tsopano tangopenyani apa ndi kuwona ungwiro wake, paliponse pamene inu mupita. Ngati ine ndingakhoze kuyima apa ndi kulankhula zinthu zomwe zawululidwa mu chipinda icho, ine ndikukuwuzani inu, izo zikhoza kusambiritsa mitu yanu mozungulira. Koma inu mukachita bwanji izo, pamene inu muli nacho chinthu chonse apa?

⁷⁵ Ndiyeno iwe, mwinamwake china, pamene iwe uchoka kwa anthu, ndiye icho chimayamba kutsegula zinsinsi. Ndiye iwe umapenya zinthu zomwe iwe sungayesere kuzinena kwa anthu,

nawenso. Chifukwa, inu mukuwona, ngati izo zikanakhala, iwo akanayamba timalingaliro tating'ono.

⁷⁶ Ndiyeno tiyeni tiwone chomwe kamphatso kakang'ono ka machiritso aka kachita, momwe iko kanasokonezera mpingo. Aliyense anali nako kugirigisha, aliyense anali nacho *ichi*; ndipo pansu pomwe mu mtima mwanga, (Mulungu akudziwa ndizo zowona), ine ndinadziwa kuti sizinali zolondola, chifukwa Iye anandiwuza ine choncho. Mukuwona? Koma ndiko kuchita mowonera kwake kwabodza, kuti angowaponyera anthu kumbali. Tsopano, uko nkulondola. Tsopano, koma, inu mukuwona, iwe sungakhoze kunena zinthu zimenezo. Kulibwino kungozisiya izo zokha.

⁷⁷ Ndipo inu mukukumbukira Chikoka Chachitatu? Iye anati, “Usati uwuze aliyense.” Ine ndinati chinali chiyani icho? Ndi angati akukumbukira zimenezo? Ndithudi. Kumbukirani, nditayima pamenepo, kuyesera kulowetsa chingwe icho mu nsapato yaying'ono ija, mu masomphenya? Iye anati, “Iwe sungakhoze kuwaphunzitsa makanda a Chipentekoste zinthu zauzimu.”

⁷⁸ Ine ndinati, “Ichi chidzakhala Chikoka Chachitatu, ndipo Icho sichidzaziwika, kotero ndithandizeni ine, mwa chisomo cha Mulungu.”

Tsopano—tsopano, ife tiri—ife tiri mmusi kumene pa nthawi yotsiriza tsopano. Izo sizitenga nthawi yayitali kwambiri mpaka Mpando Wachifundo udzakhala Mpando Wachiweruzo. Pamene inu mukuwona zinthu izi zikubweramo, ndipo anthu awa akubweramo, kuli bwino inu mulowe mkati, inunso, ngati inu simuli kale mkati. Mukuwona?

⁷⁹ Tsopano, “Kusonkhanitsidwa mu malo Ammwambamwamba,” mwawona, icho chimatanthawuzanso kuposa kumangosangalala. “Mu malo Ammwambamwamba,” ngati inu mwasonkhana kwenikweni mwa Khristu, ndi chinthu chowopsyetsetsa.

⁸⁰ Kuyima pambali pa...Mngelo wa Ambuye uja, inu mukuganiza ungamangofuwula ndi kukuwa. Izo, izo sindizo izo. Icho chimakuwopsyeza iwe kwa imfa, pafupifupi. Mukuwona? Kotero, inu mukuwona, apo—pali kusiyana mu kukondwerera chabe ndi kuvina kolumphalumpha, komwe kuli konse kwabwino, ndiyeno kubwera mmusi ku chinthu chenicheni. Mukuwona? Mukuwona? Apo mpamene pali mantha. Ndicho chinthu chowopsya. Osati kuti iwe umawopa kuti watayika; koma kwenikweni pamaso pa Umunthu waungelo, ndi Mzimu Woyera Mwiniwake atayima pamenepo.

⁸¹ Tsopano, ilo lidzakhala gawo la Mkwatibwi. Ndilo lomwe lidzapite kukalipanga ilo, mwawona, onse awo omwe agona. Ndipo kodi ife sitingawone mwamtheradi. . .

[Chojambulira matepi chilephera. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...tikupemphera tsopano kuti Inu mupereke machiritso a anthu, kupyolera mu mipango iyi, ndasanjikapo. Mu Dzina la Yesu. Amenii.

Tsopano, kodi ziribwino tsopano? [Abale ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Zikomo inu. Winawake waponda pa chinachake? [M’bale ati, “Tiri nawo marekoda ochuluka kwambiri pa nthambo iyo.”] Marekoda ochuluka kwambiri amayika kupsyinjika kochuluka pa iwo. Mukuwona? Chabwino, kumangosinthana. Kungotenga tepi ndi kusintha tepi, ndi kudzapanga kuchokera kwa iyo. Tsopano, zindikirani tsopano funso lotsatira.

174. Kodi avangeri azipitirira ku minda?

⁸² “Mu ora lino,” zedi, zomwe iwo akutanthawuza. Ndithudi, mwa matanthauzo onse. Musati musinthe kanthu. Ngati Yesu akubwera mmawa, lalikirani lero monga ngati izo zikanati zikhale zaka khumi kuchokera lero, koma khalani moyo monga ngati izo zikhala pa ora lino.

⁸³ Musati—musati musokonezedwe tsopano. Ndicho chimene ine ndikuyesera kukuchenjezani inu nacho, mwawona. Kokha musati mukhale osamvetseka, achirendo. Musati musinthe kanthu. Koma ngati inu mukuchita chinachake cholakwika kapena kuchita choyipa, lapani, mwawona, bwererani kwa Mulungu. Pitirirani pa utumiki wa uvangeri wanu basi monga inu mumachita nthawizonse.

⁸⁴ Ngati inu mukumanga nyumba, ikwezenibe iyo. Yesu akubwera mawa, inu mupezedwe wokhulupirika pa ntchito. Ngati inu mukumanga tchalitchi, pitirizani, chikwezeni icho. Ine kulibwino ndiziyika ndalama zanga mu chinachake monga icho, kuposa kuti ndidzapezeke ndi ndalama mu thumba mwanga. Mwawona?

⁸⁵ Kotero basi—muzingopirirabe, pitirizani momwe inu muliri. Aliyense akumvetsa tsopano? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Zipitiriranibe, ndipo muzingopitirirabe momwe inu muliri. Tsopano, basi—musangoti muyime. Musati muchite kanthu... Muzingopitirirabe basi momwe inu muliri. Pitirirani kumutumikira Ambuye.

⁸⁶ Tsopano, mwa chitsanzo, ngati inu munali—ngati inu munali kumugwirira ntchito munthu, ndipo inu munadziwa kuti anali maminiti khumi ndi asanu isanakwane nthawi yowerukira. “Chabwino,” inu mukanati, “ha, maminiti khumi ndi asanu okha atsala, kotero ine ndikhoza kungopita ndi kukakhala pansii.” Iwe ukhoza kuchotsedwa chifukwa cha maminiti khumi ndi asanuwo.

⁸⁷ Ngati inu mukubzala tirigu; bzalani tirigu wanu. Inu mukukumba mbatata; pitirirani, zikumbeni izo. Mukuti, “Chabwino, palibe yemwe ati adzadye izo”? Izo sizikupanga

kusiya kulikonse. Kazikumbeni izo, chonchobe. Mukuwona? Eya. Ingomapitirirani monga inu muliri.

⁸⁸ Ine ndinalandira kalata kuchokera kwa winawake tsiku lina. Winawake anawawuza iwo, anati, “Chabwino, nthawi ili pafupi. Kagulitseni munda. Tsopano inu simusowa chakudya chomwe inu mumakhalira nacho moyo, pa farmu,” anati, “chifukwa Zakachikwi izi ziyamba, ndipo inu simuchisowa icho. Kotero inu mungopitirira. . . Ndipo pamene nthawi ya Chisawutso ikupitirira, ana ako sanapulumsidwe, kotero ingowasiyira iwo. . . Kuwalola—kuwalola anawo akhale nayo farmu, kumene iwo angakhoze kudya za iyo, koma inu nonse mugulitse munda wanu,” ndi—ndi, kapena chinachake monga choncho. Ndipo, o, iwo anamvera izo. . .

⁸⁹ Ine ndinati, “O, mai!” Ngati ine ndikanadziwa kuti Iye akubwera mawa, ndipo ine nkukhala mulimi, ine ndikanabzala mbewu zanga lero. Ndithudi. Ngati Iye anandipanga ine mchikembe, ine ndikangokhala pa ntchito yanga kumene. Uko nkulondola. Ngati Iye anandipanga ine makaniki, anati yemwe. . .

⁹⁰ Winawake anati, tsiku lina, iye anati, “Mzanga anabwera muno ndipo anati, ‘Nnena, m’bale, iwe ukudziwa chiyani?’ Iye anati, ‘Ine ndikupatsa iwe seti yachiwiri ya makiyi. Ine ndagula galimoto yatsopano.’ Iye anati, ‘Ine ndikupatsa iwe seti yachiwiri ya makiyi,’ ankamuwuza m’busa wake. Anati, ‘Ine ndikupatsani inu seti yachiwiri ya makiyi, chifukwa Mkwatulo ukhoza kubwera, inu mukudziwa, ndipo,’ anati, ‘ine sindidzayisowanso iyo konse.’” M’busa anali woti awuphonya iwo, inu mukuwona. O! Uko nkukonzekera, sichoncho? Chabwino. Koma ndimo—ndimo momwe ziliri, mwawona, ife sitikuyenera kukhala mwanjira iyo.

⁹¹ Ife tiyenera kukhala a—osasokonezeka, Akhristu olimba, mwawona, kuti ine ndayikidwa pano kuti ndikagwire ntchito mpaka ku miniti yotsiriza. Ine ndiri nayo ntchito yoti ndiyichite, ndipo ine ndidzapezeke kumene wokhulupirika pa malo a ntchito. Ngati Iye akubwera mmawa uno, ine ndikufuna ndikhale nditayima pomwe pano mu guwa.

⁹² Inu mukuti, “M’bale Branham, ngati Iye anali woti abwera mmawa uno, simukuyenera inu kukakhala muli kunja *uko?*” Ayi, bwana!

⁹³ Awa ndiye malo anga a ntchito. Ine ndidzakhala ndikuyimirira pomwe pano, ndikulalikira, pamene Iye akubwera, ndikunena zinthu zomwezo zimene ine ndikunena. Ndiye, pamene Iye akubwera, ine ndidzangosuntha kutuluka naye Iye, mwawona.

⁹⁴ Ngati ine ndikulima mbatata, ine ndidzakhala ndikulimabe, molimbika basi monga ine ndingathere. Pamene Iye akubwera, ine ndidzangosiya khasu ndi kunyamuka kupita.

Mukukumbukira mu chaka chachisangalalo? Ngati iwo anali khasu—akulima ndi khasu, iwo amangopitiriza kumalima. Iwo ankadziwa kuti chaka chachisangalalo chinali mwina maminiti khumi otsatira, ndipo lipenga liwomba pa chaka cha chisangalalo. Iwo amangopitirizabe kukonza msipu, chirichonse chimene iwo anali kuchita. Koma pamene lipenga linawomba, ndiye iwo ankagwetsa chokonzero msipu, ndi kumapita. Mwawona, ndi zimenezo, amangopitirirabe kukweza udzu mpaka lipenga litawomba. Chabwino.

[Phokoso likumveka kuchokera ku chinachake chapafupi—Mkonzi.] Funso, “Molingana ndi kutsegula...” Kodi izo... Chinachake chachitika? Ha? Icho—icho chinapanga phokoso pamwamba apa. Funso:

175. Molingana ndi kutsegula kwa Chachisanu—Chisindikizo Chachisanu, Mose ndi Eliya ali—ayenera kufa. Nanga bwanji Enoki?

⁹⁵ Ine sindikudziwa. Mukuwona? Ine—ine...Ngati ine sindikudziwa, ine ndingokuwuzani inu kuti ine sindikudziwa. Mukuwona? Ine—ine sindiri—ine sindikudziwa mayankho onse, anthunu. Ine—ine sindikudziwa. Ndipo ngati ine sindikudziwa, ine ndikuwuzani inu kuti ine sindikudziwa. Ngati ine ndikudziwa...Ine sindikuwuzani inu mpaka ine nditadziwa, mwawona. Koma ine—ine sindikudziwa.

⁹⁶ Ine kawirikawiri ndakhala wodabwa za izo, inemwini. Panali Enoki...Ine ndikumuwona Mose akubwera, ndipo Eliya akubwereranso, ndipo iwo akuphedwa, mwawona, koma tsopano Enoki anasinthidwa isanakwane nthawi. Ine kawirikawiri ndaganiza, ndi kudabwa, inemwini, “Chabwino, chiyani, nanga bwanji zimenezo?”

⁹⁷ Koma, ndiye, apa pali chitonthozo chokha chomwe ine ndingakhoze kunena, chiri ichi. Tsopano zindikirani, Mose anatumikira Mulungu zaka makumi anayi kokha. Mukuwona? Iye anali i—iye anali zana ndi makumi awiri. Koma zaka makumi awiri...Zaka makumi anayi zoyamba, ine ndikutanthawuza, iye anali kutenga maphunziro ake. Nkulondola uko? Zaka makumi anayi zachiwiri, Mulungu anali kuwachotsa iwo mwa iye. Ndipo zaka makumi anayi zachitatu, iye anatumikira Mulungu. Mukuwona? Chabwino. Koma Enoki anayenda zaka mazana asanu pamaso pa Mulungu, ndipo analibe chomutsutsa.” Mukuwona? Mukuwona? Koteru, Mose akubwereranso kudzatamikira nthawi yinanso yowonjezera; iye ndi Eliya.

⁹⁸ Tsopano, izo, ine sindikunena kuti izo nzolondola, mwawona. Ine ndangokupatsani inu izo kwa ganizo, mwawona. Koma kunena chabe gawo lake, ine sindikudziwa. Ine kwenikweni sindingakhoze kukuwuzani zomwe—zomwe zinachitika pamene, kapena chomwe Mulungu ati adzachite.

176. Ndi chiyani d—dzina la . . . lomwe liti lidzakhale pa anthu a Chivumbulutso 3:12?

⁹⁹ Ine—ine sindikudziwa. Eya. Iye anati, “Adzawapatsa iwo dzina latsopano.” Ine—ine—ine sindikudziwa chomwe ilo liri, mwawona. Ilo mwinamwake likadziwika pamene ife titi tikafike uko, koma ine—ine sindikudziwa chomwe ili liri tsopano, mwawona. Mukuwona, Iye akachita zimenezo. Mukuwona? Iye akuwapatsa iwo dzina latsopano lomwe—lomwe iwo akungolidziwa, iwoeni. Mukuwona?

177. Tsopano, M’bale Branham, kodi liripo Lemba lirilonse lololeza chikwati chitachitika chilekano? Ili liri lofunikira kwambiri.

¹⁰⁰ Ilo likuti, “Lofunikira.” Chabwino, ndicho chifukwa. . . Ilo silinali lokhudzana ndi izi. Momwe ine ndingakhoze kuwonera, m’bale wanga, kapena mlongo, aliyense yemwe angakhale, palibe, pokha mzakoyo atamwalira. Chifukwa, Baibulo linati, “Ife tiri omangika kwa iwo malingana ngati iwo akhala moyo.” Mukuwona?

¹⁰¹ Koteri, monga—ponena za “Lemba lirilonse?” Ndicho chomwe chinafunsidwa apa, “Kodi liripo Lemba?” Mukuwona? “Kodi liripo Lemba lirilonse?” Osati limene ine ndingakhoze kulipeza, mwawona, osati limene ine ndingakhoze kulipeza.

Chifukwa, Paulo ananena kuti a—anthu okwatirana, “Ngati mzakeyo wamwalira, ndiye iwo ali mfulu ndiye kukwatira aliyense yemwe iwo angamufune mwa Ambuye.” Koma mpaka pamenepo, koma, yang’anani, inu mutenge icho, “Mpaka imfa ife tidzalekana.” Ndicho icho. Inu mwachita kale lumbiro pa icho, inu mukuwona.

¹⁰² Koteri, ine sindikuganiza kuti liripo. Tsopano, ngati liripo. . . Ngati inu munapeza lina, ndipo liri molondola, bwanji, zonse—chabwino. Koma, kunena za inendekha, ine—ine sindikupeza lirilonse.

178. Kodi “ona iwe kuti usawononge mafuta ndi vinyo” zikutanthawuza chiyani, mu Chivumbulutso 6:6?

¹⁰³ Ndi Mzimu Woyera. Mukuwona? Ife tangopyola kumene zimenezo. Mwina winawake, inu mukudziwa, anabwera muno mochedwerapo kwa Uthenga, iwo. . . chabwino, kwa matepi ena, inu mukuwona.

“Usawononge mafuta ndi vinyo.” Kodi mafuta ndi vinyo zikutanthawuza chiyani?

¹⁰⁴ Mafuta, monga ife tinatengera mu chophiphiritsa, amatanthawuza Mzimu Woyera. Mukuwona? Vinyo ali. . . ndi mafuta, ziri zolumikizidwa palimodzi, mu Baibulo, mu kupembedza. Mukuwona? Ndipo vinyo, monga ife tinayikira, ndiko komwe ine ndinapezera lingaliro, “Kukondowedwa.” Vinyo amakondoweza. Ndipo vinyo, mu chake—choyimiridwa

chake cha chilengedwe chake, kuchokera ku kukondoweza, ali vumbulutso.

¹⁰⁵ Tsopano ingoganizani. Nchiyani chomwe chimakondoweza Mpingo? Vumbulutso. Mwawona? Kotero, vinyo, vinyo watsopano, akanakhala... Tsopano yang'anani. Mafuta ndi vinyo zinkapita pamodzi, mu nsembe; zinkapita pamodzi, mu—mu kupembedza kwa mpingo. Tsopano zindikirani, kusunghanitsidwa pamodzi, kulumikizidwa pamodzi.

¹⁰⁶ Ngati inu muli nalo bukhu la kufotokoza, inu muyang'ane ndi kupenya mndandanda wonse pamene vinyo ndi mafuta zakumana pamodzi mu kupembedza. Ngati inu muli nalo la—la Cruden, bwanji, ilo limanena mmenemo.

¹⁰⁷ Tsopano zindikirani pa izi. Koma tsopano, inu mukuwona, mafuta ali nthawizonse Mzimu Woyera. Ife tikuzipeza zimenezo cha mu Ezekieli. Ndipo ife tikuzipeza izo mu Chipangano Chakale. Ife tikuzipeza izo monse kupyola mu Chipangano Chatsopano.

¹⁰⁸ Nchifukwa chiyani ife timawadzoza odwala ndi mafuta? Ife timawadzoza odwala ndi mafuta chifukwa icho chimaphiphiritsa kutsanulira kwa Mzimu Woyera pa iwo. Mukuwona? Ndiponso, anamwali ochenjera anali nawo Mafuta; opusa analibe Mafuta, Mzimu, mwawona. Tsopano, awo ndi Mafuta. Ndiyeno vinyo, iye—ali... Ngati mafuta amayimira, amayimira Mulungu. Mulungu ndi Mzimu. Mukuwona?

¹⁰⁹ Mulungu ali Mawu. “Pachiyambi panali Mawu; Mawu anali ndi Mulungu. Mawu anapangidwa thupi, ndipo uyo anali Mulungu.” Tsopano, ndiye, ngati Mawu tsopano mu... akukhala apa mu mawonekedwe achibadwa tsopano, vinyo ali ngati madzi, amene, kapena vumbulutso lomwe limawulula kumasulira kwa Mawu uko, lomwe limamukondoweza wokhulupirira, inu mukuwona. Mai, iwo amangonena kuti, “Ine sindinachiwonepo Icho kale konse! Mai! Ulemerero!” Ndicho chiyani? Mwawona, kukondoweza, mwawona, kwa vumbulutso.

¹¹⁰ Ine sindinkadziwa izo mpaka tsiku lina, nditakhala pamenepo, ngakhale. Mukuwona? Tsopano, ndicho, “Nchiyani chomwe mafuta ndi vinyo...” Izo zinali, “Ona kuti iwe usawononge ayi.” Ameneyo anali wokwera pa kavalo wakuda. Ndipo iyo inali nthawi ya m'badwo wamdima, m'badwo wachitatu wa m—wa mpingo. Zindikirani. Ndipo, mkati umo, “Muli basi pang'ono pokha a Izo zatsalira, pang'onong'ono pokha, koma usawononge Izo.”

¹¹¹ Ndipo ine ndikukhulupirira ngati inu mukatenge icho, c—Chisindikizo Chachitatu, pa tepi, inu mudza... inu mukanzipeza izo mmenemo, pamene ife tinafotokoza izo mwamadongosolo, kapena mwadongosolo, kani.

179. M'bale Branham, kodi Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, ndi Bukhu la Moyo, ndi Bukhu lomwelo?

¹¹² Zedi, mwawona, chifukwa muli momwe chiwombolo chonse chalembedwamo, mu Bukhu ili. Mwawona? Maina awo ali mwa Ilo. Inu mukuti, “Chabwino, dzina lathu lalembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, M’bale Branham. Ine—ine ndinalilembetsa ilo pa, usiku wina.” Ayi, inu simunatero. Ayi, inu simunatero. Inu munangopeza kuti ilo linali Pamenepo, usiku wina, mwawona, chifukwa maina awo analembedwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Mukuwona? Ndicho, ali onse Bukhu lomwelo, mwawona.

180. Tsopano, M’bale Branham, kodi nzowona kuti—kuti Myuda aliyense, wobadwa kuyambira pamene Khristu anabwera, adzapulumutsidwa? Ndipo ali ndani zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi? Kodi ali iwo amodzi okonzedweratuwo kuti asindikizidwe nawo Mzimu Woyera? Ndipo ntchito yawo ndi yotani?

¹¹³ Pali pafupi mafunso atatu mwa limodzi, apo. Koma, apa, limodzi loyamba:

Kodi—kodi nzowona kuti Myuda aliyense wobadwa kuyambira pa Khristu, yemwe anabwera mu dziko, ndi woti adzapulumutsidwa?

¹¹⁴ Ayi. Palibe kanthu kati kadzapulumutsidwe, iwo okha omwe maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko asanakhazikitsidwe, Myuda kapena Mmitundu. Mukuwona? Ndizo zonse. Bukhulo lagwirizira chinsinsi chimenecho, ndipo Bukhulo likungofutukula izo tsopano; osati dzina la mmodzi aliyense, koma chomwe chinsinsi cha Bukhulo chiri, pamene ali kuyitana maina amenewo. Inu potsiriza mwamvetsa zimenezo tsopano? Mukuwona?

¹¹⁵ Bukhulo silikunena, “Tsopano, Lee Vayle ndi woti adzapulumutsidwa mu nthawi ya m’badwo wa mpingo uwu, kapena—kapena Orman Neville,” kapena—kapena aliyense. Ayi, ilo silikunena zimenezo. Ilo likungosonyeza chinsinsi, kufutukula chinsinsi cha chomwe chinthucho chiri. Koma ife, eniathu, mwa chikhulupiriro, timakhulupirira Izo. Ndicho chimene ine ndinanena usiku wina.

¹¹⁶ Winawake anati, “Chabwino, apo palibe chifukwa mwa ine kumayesera izo. M’bale Branham anati pakhala mmodzi yekha ati adzapulumutsidwe kuchokera mu Jeffersonville.” Mukuwona? Tsopano, mwawona, ziri kusonyeza fanizo. Izo—izo—izo siziri, izo—izo siziri izo. Pakhoza kukhala zikwi zopulumutsidwa. Ine sindikudziwa. Ine ndikuyembekeza mmodzi aliyense wa iwo wapulumutsidwa, mwawona, koma ine sindikudziwa.

Koma apa pali njira yomwe ine ndikufuna kukhulupirira izo, “Ndine mmodzi ameneyo.” Inu mukhulupirire mofanana kwa inu. Ngati inu simutero, ndiye pali chinachake cholakwika

nacho chikhulupiro chanu; inu simuli otsimikiza chomwe inu mukuchita.

117 Inu mungakhoze bwanji—inu mungakhoze bwanji kuyenda apo pamaso pa imfa, pamene inu simuli otsimikiza kwambiri ngati inu muli wopulumutsidwa kapena ayi? Mukuwona? Inu mungakhoze bwanji kupita mmusi apa ndi kukanena kwa munthu wopuwala uyu wagona apa, wakhungu ndi wopotokapotoka, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Nyamuka! Yesu Khristu wakupanga iwe wathunthu”?

118 Inu mungakhoze kuyima bwanji, thupi lozizira lowuma kale ilo litagona apo, lomwe lamwalira, ndipo lakhala lakufa kwa maora ndi maora, ndi likugona pamenepo, lozizira ndi lowuma; ndi kunena, “PAKUTI ATERO AMBUYE, nyamuka ku mapazi ako”? Iwe kuli bwino, iwe uyenera kudziwa chomwe uli kuchilankhula. Mwawona?

119 Chabwino, nkumati, “Imfa imatenga chirichonse. Zonse zapita.” Eya, koma pamene Mawu a Mulungu awululidwa, ndipo iwe ukudziwa kuti ndi Mulungu, izo zimasintha zinthu. Ndiko kulondola.

120 Tsopano, inde, Ayuda awa sali...Osati Ayuda onse adzapulumutsidwe. Ayi, bwana. Iwo sadzapulumutsidwa; iwo okha omwe...Pamene Iye akulankhula za—za Myuda, “Myuda,” monga dzina chabe lomwe linapatsidwa kwa iwo pamene iwo anachoka...Ine ndikukhulupirira, Nebukadinezara, uko, anayamba kuwacha iwo “Myuda,” poyamba, chifukwa fuko la Yuda linatengedwa kumeneko. Ndipo iwo anapatsidwa dzina la “Myuda,” tsopano, chifukwa iwo anabwera uko kuchokera ku Yudeya, ndipo iwo anatenga dzina la Myuda.

121 Koma, tsopano, Israeli ali wosiyana. Israeli, ndi Myuda, ziri pamodzi zosiyana. Myuda aliyense—Myuda aliyense sali Muisraeli, mwawona. Ayi, iye ali chabe Myuda. Koma, ndiye, Israeli...Paulo sananene konse kuti Ayuda onse adzapulumutsidwa. Iye anati, “Israeli yense adzapulumutsidwa.” Chifukwa? Dzina la Israeli, ndilo—ndilo dzina la chiwombolo, njira yonse mmbuyo. Mukuwona? Ndipo Israeli yense adzapulumutsidwa, koma osati Yudeya yense—Chiyuda kuti chidzapulumutsidwa. Mukuwona?

122 Monga ngati Amitundu, padzakhala pali...Alipo zikwi kuphatikiza zikwi za—za anthu, inde, mamilioni kwenikweni, mu mabungwe awa, ndipo iwo amawatcha “Akhristu, mpingo wa Khristu,” ndi mayina onse ngati awo. Icho sichitanthawuza chinthu chimodzi. Ayi...Icho sichikutanthawuza kuti iwo adzapulumutsidwa.

Anthu amati, “Tsopano, iwe uyenera kukhala wa *ili* kapena *ilo*, bungwe, bungwe linalake. Ngati dzina lako siliri pa bukhu lathu, iwe watayika.” Tsopano, uwo ndi mwambo. Mwawona? Uwo ndi mwambo. Mwawona?

123 Pali njira imodzi yokha yomwe iwe ungakhoze kupulumutsidwira, ndipo, iyo ili, “Osati iye amene afuna, kapena iye yemwe athamanga, iye yemwe...Ndiye, ali Mulungu Yemwe amawonetsa chifundo.” Ndipo Mulungu, mwa kudziwiratu Kwake, anawukonzeratu Mpingo kwa ulemerero Wake, ndipo ndiwo amodzi omwe akupulumutsidwa. Kulondola. Tsopano, chikhulupiriro chanu chiri chomangika kwambiri Pamenepo!

124 Inu mukuti, “Chabwino, chikhulupiriro changa chiri chomangika Pamenepo.” Ndipo penyani mtundu wa moyo womwe inu mukukhala. Inu mukuwona inu simuli ngakhale wokwanira kwa Pamenepo. Nangula wanu ali wolakwika. Inu mwamuyika iye pa mchenga mmalo mwa thanthwe. Funde pang’ono loyamba liponyera iyo kumbali. A-ha.

125 Mawu akati akhale atawululidwa mu chinachake. “Mpingo wanga sumaphunzitsa Zimenezo!” Izo zikusonyeza pomwepo kuti inu munalibe nangula pa thanthwe. Inu munali mu mchenga. A-nha. Ndiko kulondola. Kotero, tsopano inu mukuwona, tsopano.

Ndipo zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, kodi ali iwo amodzi okonzedweratu?

126 Inde, bwana. Ameneyo ali Israeli, Israeli wauzimu.

127 Tangoganizani, padzakhala mamiloni a iwo mmenemo. Ine sindikudziwa kuti alipo angati mmenemo tsopano; ine ndikuganiza gulu lonse, koma iwo onse sadzapulumutsidwa chifukwa iwo ali mu Yudeya. Mukuwona?

Kodi inu muli nalo lingaliro la angati omwe ali kumeneko tsopano? Ine sindikudziwa. Koma iwo ali mwinamwake... Kuzunza uku kotsatira kukayamba kuwuka... Iwo akuchulukira mwa... Inu mukudziwa, ine ndiri nayo tepi pa iwo, ndikuyitengera kumadzulo tsopano ku—ku umodzi wa m—m—mpingo wa Chipangano umene uli ku... .

128 Uli chabe wakale...O, ine ndayiwala tsopano. Iwo unayamba...Iwo ali nawo umenewo komwe uko mu Afrika. Dutch Reform. Ndi mpingo wa Dutch Reform, uli wa Chipangano. Tsopano, ngati alipo yense wa inu mwakhala apa, ine ndikuwuzani inu chifukwa chake. Inu mukugwirabe kwa Katekizimu wa Heidelberg wakale uja, ndipo ndicho chimodzimodzi chifukwa chomwe mwatsalirabe mu... mukanali Dutch Reform. Kotero, inu mukhoza kupukuta ndi dzina la Chimereka. Ndicho—ndicho chinthu chiri kuseri kwa iwo, chifukwa inu mukuphunzitsa kuchokera mu katekizimu yemweyo, wa Heidelberg wakale. Inu mukawafunse abusa anu ngati izo siziri zolondola. Mukuwona? Kotero, tsopano, muzindikire ichi.

Zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, iwo ndiwo amodzi okonzedweratu kuti adzasindikizidwe nawo Mzimu Woyera?

¹²⁹ Inde, bwana. Ndizo chimodzimidzi zolondola. Chabwino. Tsopano ngati pali aliyense . . . Tsopano ngati ndiri . . .

Ngati ine sindinayankhe, mokukwanirani inu, bwanji, mwinamwake ndiri . . . ine ndikhoza kulakwitsa, mwawona. Koma, ichi, ndimo mwakukhoza kwa chidziwitso changa, inu mukuwona. Ichi chiri mwakukhoza kwa chidziwitso changa.

181. M'bale Branham, monga inu mwatsawutsidwira kapena kuts- . . . pa mbewu ya serpenti . . . (A-ho, ine sindinalizindikire limodzi ili. Limodzi ili linandipulumuka ine) . . . mbewu ya serpenti sabata yino, kodi chingakhale mwadongosolo kufunsa funso ili? Amzanga andifunsa ine kuti ndifotokoze Genesis 4:1, ndipo ine sindingathe. Kodi inu mungandithandize ine?

¹³⁰ Liri—liri kumbali kwa phunziro. Koma, chonchobe, ndi—ndi—ndiyesa mwakukhoza kwanga, mwa thandizo la Mulungu. Tiyeni tiwone tsopano. Ndiroleni ine ndipukutepo, kwa pang'onong'ono chabe. Ine ndikuganiza ndipo pomwe iye anati, “Ine ndalandira mwana kuchokera kwa Ambuye.” Ine—ine ndikukhulupirira icho chiri. Ine ndikuganiza Eva ananena zimenezo pamenepo. Ine ndati ndifufuze, ndikhale wotsimikiza.

¹³¹ Chifukwa, ine ndinanena, usiku wina, asanu ndi awiri . . . mmalo mwa . . . mazana asanu ndi awiri mmalo mwa zikwi zisanu ndi ziwiri. Kotero izo zimandipangitsa ine manjenje kwambiri, mwawona, ndipo iwe ukungomayenera kukhala woyang'anitsitsa. Ndipo mdani pa mbali iliyonse, ndipo iwe—iwe uli ukudziwa zimenezo, inu mukuwona. Inde, ndizo izo.

Ndipo Adamu anamudziwa mkazi wake Eva; ndipo iye anayima, ndipo anabala Kaini, ndipo anati, Ine ndalandira munthu kuchokera kwa Ambuye.

¹³² Tsopano, ine nding'okuyankhani inu funso, m'bale wanga, kapena mlongo. Ndipo tsopano, kumbukirani, osati—osati kuponyera kwa inu, ayi. Ine ndikuyesera kukuthandizani inu, mwawona. Ine ndimakukondani inu, ndipo ine ndikuwakonda anthu omwe mwina akanakhala otsutsa pa icho. Koma ine sindikuganiza munthu uyu ali wotsutsa. Iwo anati, “Mundithandize ine,” mwawona, chifukwa anthu akukhulupirira izo, koma iwo basi sali oyikidwa mokwanira, ndi Mzimu, kuti adziwe choti anene kwa anthu omwe awafunsa iwo izo.

¹³³ Tsopano, iye akunena apa chomwe funsola liri, mosakayika, kuti iwo akunena kuti, “Eva anati analandira munthu uyu kuchokera kwa Ambuye.”

134 Inu mukuganiza moyo ukanakhoza kubwera chotani konse ngati iwo ukanati usabwere kuchokera kwa Ambuye, kaya iwo ukhala wolondola kapena wolakwika? Ndani anamutumiza—ndani anamutumiza Yudas Isikarioti mu dziko? Mundiwuze ine izo. Baibulo linati iye anabadwa “mwana wa chitayiko.” Mukangowafunsa iwo limodzi ilo; zikakhala ngati mbodzi mu ndimu, mwawona. Mukuwona? Tsopano, inu mukuwona, iwo sangakhoze—sangakhoze . . . Izo ziri.

135 Zindikirani, ndiye, ngati inu mukufuna kuwatengera iwo kanjomba kakang’ono mochulukira. Penyani. Eva analankhula apa, ngati inu mukufuna kutenga izo mu chilankhulo ziri apa, chomwe chalembedwa koteru chiri chobisidwa kwa diso, anzeru ndi aluntha. Eva, apa, momwe izo zaphunzitsidwira, kuti Mulungu anali Mmodzi yemwe iye anabalilako mwana uyu. Ndipo Iye ali Mzimu, ndipo sangakhoze kuchita icho. Mukuwona? Tsopano yang’anani apa, ngati inu mukufuna kuzindikira icho. “Ine ndalandira—munthu kuchokera kwa Ambuye.” Mwawona, inu simungachipange icho kumveka mwina . . . Koma icho chiyenera kukhala nako kutanthawuzira kolondola, mwawona. Inde, bwana. Ayi, bwana, ngati icho, ndiye mzimu . . .

136 Ndipo ife nthawizonse timatsatira chikhalidwe cha kholo lathu. Inu mukudziwa zimenezo. Penyani pa mwanayo, chibadwa. Chabwino, ndiye, Adamu anali mwana wa Mulungu; Eva anali mwana wamkazi wa Mulungu; kulondola, chinthu choyamba cha chirengedwe cha Mulungu, chomwe sichikanakhoza kukhala nako kachitsotso kamodzi ka—ka choyipa paliponse pa za izo. Choyipa sichinali ngakhale kudziwika.

137 Ndiye bwanji Kaini anali wabodza, wakupha, ndi china chirichonse? Kodi zimenezo zinachokera kuti? Ingodzifunsani nokha funso limenelo. Iyo inali mbewu ya serpenti. Mukuwona? Kodi Baibulo silimanena choncho? Iyang’aneni mbewu yake njira yonse mpaka mmusi. Mwa iyo, iye anakhala . . .

138 Kodi dziko liri la yani? Mdierekezi. Ndani akuliramulira ilo tsopano? Mdierekezi. Kulondola chimodzimodzi. Mdierekezi akulamulira dziko. Iye anamuwuzwa Yesu, anati, “Wawona momwe liriri lokongola, ulemerero wonse? Ine ndilipereka ilo kwa Iwe ngati Iwe utandipembedze ine.” Mwawona, iye ali wolamulira wa ilo. Tsopano ilo liri lake.

139 Tsopano yang’anani, ana ake ali anzeru; ana a Mdierekezi. Kapena, tengani ana a Kaini, ngati inu mukufuna kutero, ndipo abweretseni iwo kudutsa kumene kupyola mmibadwo, ndipo inu mupeza kuti iwo anali anthu ophunzira, mmodzi aliyense wa iwo.

140 Koma ndiye pamene iye anamupha Abele; ndipo Mulungu anamubwezera iye Seti, anali choyimira cha wolungama,

kuti awombole; pokhala atafa, ndi kuwuka kachiwiri. Ndipo kuchokera pamenepo. . . Tsopano yang'anani. Osati kuchokera kwa mbewu yoyamba, ya chibadwa; iwo anafa. Tsopano inu mwatseguka malingaliro anu? Mukuwona? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mbewu yoyamba, ya mbewu ya chibadwa, yabwino mwawamba chabe, iyo inayimira mpingo wamakono, Abele. Pofuna kuti asunge mzere umenewo kubwera mmusi, mmodzi uyo anafa kotero wina akanakhoza kuwuka, inu mukuwona. Kotero, kuyenera kukhala kubadwanso, kachiwiri. Inu mwachigwira icho? ["Ameni."] Chabwino, basi choncho inu mwamvetsa izo, mwawona. Mukuwona?

¹⁴¹ Ndi zimenezotu, choyimira changwirowo. Kotero ngakhale munthu wachibadwa, wobadwa kwa—kwa Adamu, abambo ake, akuwonetsa kachitidwe ka chibadwa kaja. Sizingagwire ntchito; munthu wachibadwa sazindikira zinthu za Mulungu. Kotero apo panali Munthu anabwera mwachibadwa, ndipo anafa, pofuna kuti akabwezeretsenso izo kachiwiri; ndipo iye akuyimiridwa mu imfa ya—ya—ya Abele, ndi kulowezedwa ndi—ndi Seti.

¹⁴² Ndipo yang'anani anali anthu a mtundu wanji iwo, tsopano, mzimu uwo womwe unabweretsedwa kuchokera kwa iye; odzichepetsa, achikumbe, oweta nkhosa. Yang'anani chomwe chinabwera kuchokera ku nzeru iyi ya dziko apa; anthu ophunzira, omanga, ndi—ndipo ndi zitsulo, ndi mitundu yonse ya luntha la kuphunzira ndi zinthu. Penyani kumene iwo anatsirizira. Iwo anali kumusi uko, ndipo Mulungu anawononga mmodzi aliyense wa iwo, mmodzi aliyense wa iwo, ndipo anapulumutsa odzichepetsa. Kodi Yesu sananene, mu Mateyu 5, "Ofatsa adzalandira dziko lapansi"?

¹⁴³ Kotero, eya, musati mudandawule. Iwo alibe phazi limodzi poti ayimepo. Mukuwona? Iwo sakhulupirira uyo kukhala mwana wa Kaini. Koma ife tiri nayo tepi pa izo, ngati mukufuna kumvera izo zikufotokozedwa mwa dongosolo. Mukuwona? Ayi, bwana.

¹⁴⁴ Ndipo ine ndinawona iwo ali nacho cholemba mu pepala kumtunda uko, pamene sayansi ili tsopano kufika potsimikizira kuti "Eva sanadye konse apulo. Iye anali ndi apurikoti." Mukuwona? Ine ndiri nayo pepalayo kunyumba uko tsopano, mwawona. "Iyo inali apurikoti." Bwanji—motalikira bwanji anthu angakhoze. . . Ndiro lingaliro la chithupi, mwawona.

"Ndiye, makamaka, Mose sanawoloke madzi konse. Iye anawoloka kupyola nyanja ya mabango; anabweretsa Israeli kuwoloka pa mapeto a kumtunda kwa Nyanja Yakufa. Uko kunali mulu wa mabango kumeneko, nyanja yonse ya mabango, basi pamene panali madzi nthawi imodzi, anaphwera. Ndipo Mose anatenga njira ya chidule ndipo anapita kuzungulira njira imeneyo." Ndipo mipingo ya Orthodox inavomereza izo. Inu mwawona izo. Mipingo ya Orthodox inavomereza izo, kuti izo zinali choncho.

¹⁴⁵ O, munthu, sungakhoze iwe kuyiwona mbewu ya serpenti iyo, wotsutsakhristu uyo, ndipo chinthu chonse chitagona pomwe apo? Ndithudi. Inde, bwana.

M'bale Branham, chonde mumupempherere wamng'ono wanga...(Chabwino, ndilo pempho la pemphero; ine ndaliwona ilo.) **Mumupempherere kamdzukulu kanga kakamuna, akudwala kwambiri nacho chimfine. Iye ali mu Hotelo ya Riverview.**

¹⁴⁶ Ambuye Yesu, munthu wosawuka uyu apa sanangolemba izo pachabe. Iye anawona Inu mwadala chabe mukuchotsa ngakhale nyamakazi kuchokera kwa mnyamata wamng'ono usiku wina. Iye akuziwa kuti Ndinu Mulungu wamkulu, ndipo ife tikupereka mapemphero athu kwa mnyamata wamng'onoyo. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole kuti iye achiritsidwe. Amenii.

¹⁴⁷ Pamene winawake alemba chirichonse, icho sichiri mwachabe. Iwo—iwo—iwo ali nazo...Ziribe kanthu kaya zimveka mophweka chotani kwa ife, ndi kuchuluka chotani kwa izo, koma—koma pali chinachake kuseri kwa icho, inu mukuwona; dona uyo, mnyamata wamng'ono uyo, chinachake.

182. Kodi ali Eliya, yemwe akubwera kudzalalikira kwa Ayuda, munthu weniweni yemwe anakhala moyo pa dziko lapansi, kapena kodi iye adzakhala mzimu wa Eliya mwa munthu wina?

Tsopano, ndilo, ine—ine ndikuwopa kuti ndinene. Ine sindikudziwa. Mukuwona? Ndiroleni ine ndiwerenge ilo kachiwiri.

Kodi ali Eliya, yemwe akubwera kudzalalikira kwa Ayuda (o, inde), munthu weniweni yemwe anakhala moyo pa dziko lapansi, kapena kodi iye adzakhala mzimu wa Eliya mwa munthu wina?

¹⁴⁸ Tsopano, ngati ine ndikanakhoza kuyankha ilo molondola, ine ndikanakhoza kukuwuzani inu za Enoki, mwawona. Koma ine—ine sindingakhoze kuchita izo, mwawona. Chinthu chokhacho ine ndikudziwa chiri, basi, Lemba likunena chomwe icho chiti chidzakhale. Ndipo tsopano icho chikhoza kukhala kuti...Tsopano, ine—ndiri kukhala ngati kutsamira...Tsopano ndiroleni ine ndinene izo mwanjira iyi. Ndipo ine ndikuyembekeza tepi, abale pa matepi, adzamvetsa izi. Ine ndikutsamira kokhulupirira kuti awo adzakhala anthu odzozedwa, a mzimu wawo. Chifukwa, mwawona, iye akuti, “Kodi osati...pa Elisha? Kodi mzimu wa Eliya sukukhala pa Elisha?” Mwawona, “mzimu wa Eliya.” Ndipo iye anachita basi monga Eliya anachitira, mwawona. Kotero, ine, ngati ine...Koma ine sindingati izo nzowona. Ine—ine sindikudziwa, mwawona. Ine ndiri wowona mtima nanu. Ine sindikudziwa.

183. M'bale Branham, chonde kodi inu mungandiyankhire limodzi ili ine, la ubatizo? Mateyu 28:19 amaphunzitsa,

“Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ndipo Petro, mu Machitidwe 2:38, “mu Dzina la Ambuye Yesu.” Kusintha uku kunabwera liti mu Machitidwe a Atumwi? Tsopano, ine ndikukhulupirira, “mwa Ambuye Yesu.”

¹⁴⁹ Chabwino, m'bale kapena mlongo, yense yemwe analemba ilo, apo—apo panalibe kusintha kumene kunabwerapo, mwawona. Izo. . . Ndipo Petro anachita chimodzimidzi chomwe Yesu anati achite. Tsopano, ngati winawake abwera ndi kunena, “Gwiritsani ntchito mawudindo a Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” iwo anachita chomwe Petro anati tisachite, koma chimene Mulungu anati tisachite. Mukuwona? Tsopano, Yesu ananena kuti. . .

¹⁵⁰ Ife tidzango—kungotenga pang'ono pokha. Tiri. . . Ine ndikufuna kungokusonyezani inu chinachake apa. Zindikirani. Tsopano zindikirani, ngati inu muli apa, munthuyo. Ine ndiyika zidutswa zitatu za zinthu apa. Tsopano penyani. [M'bale Branham akukhazikitsa zinthu zitatu monga zitsanzo—Mkonzi.] *Ichi chiri Atate, ichi chiri Mwana, ichi chiri Mzimu Woyera; monga anthu a utatu amawakhulupirira iwo, amakhulupirira kuti iwo ali anthu atatu osiyana. Iwo amakhulupirira zimenezo. Mukuwona? Chabwino, ndiye, tsopano ndiroleni ine. . .*

¹⁵¹ Ndiyeno mu Mateyu 28:19. Yesu anati, “Pitani inu mu dziko lonse, ndipo kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye. . .” Ayi, ine ndikupempha chikhulukiro chanu. Ine ndikubwereza Machitidwe tsopano, kapena mu Machitidwe 2, ine ndikukhulupirira. Ayi, Luka 24:49, ine ndikubwereza. Iye anati. . . Ndiroleni ine ndiwerenge izo, ndiye ine ndazipeza izo, mwawona, ndiyeno. . . chifukwa tsiku lina ine ndinanena izo pamene ine sindinali. . . Ine ndikufuna kukhala wotsimikiza kuti ndatenga izi molondola. Ine—ine ndikuwudziwa mutu womwe inu mukuwunena pamenepo, koma ine ndikungofuna kupeza chabe zomwe Iye ananena. Tiyeni tiyambire pa ndime ya 16, wa 29. “Ndiye pamene khumi ndi mmodzi anakhala pa chakudya, a. . .”

Ndiye khumi ndi mmodzi. . . anachoka kumka ku Galileya, kumka mu phiri kumene Yesu anali atawawuza iwo.

Ndipo pamene iwo anamuwona iye, iwo anamupembedza iye: koma ena anakayika.

Ndipo Yesu anabwera ndipo analankhula kwa iwo, kunena, mphamvu Zonse mu miyamba ndi mu dziko lapansi zapatsidwa kwa. . . Mphamvu zonse zapatsidwa kwa ine mu miyamba ndi mu dziko lapansi.

¹⁵² Tsopano mphamvu ya Mulungu ili kuti? Mulungu ali kuti? Ngati mphamvu yonse ya ku Kumwamba, ndi mphamvu yonse yomwe ili mu dziko lapansi, yapatsidwa, tsopano Mulungu ali

pati? Apo Iye ali, mwawona. Ndiyo yomwe ikulankhula kwa inu. Chabwino.

Pitani inu chotero, ndi kukaphunzitsa mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.

153 Tsopano dera la a utatu la izo, “Ine ndikukubatiza iwe mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, mu dzina la Mzimu Woyera.” Izo siziri ngakhale mu Zolemba Zoyera. Mukuwona? Iye anati, “Mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la . . .” Osati mu . . . ndi kuyika dzina patsogolo pa mmodzi aliyense. Dzina limodzi! Yang’anani apa. Sananene kuti, “Mukawabatize iwo mu mayina.” D-z-i-n-a, Dzina limodzi, “Mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Mukuwona?

154 Tsopano ine ndikufuna ndikufunensi inu. Kodi “Atate” ndi dzina? [Osonkhana, “Ayi.”] Kodi “Mwana” ndi dzina? [“Ayi.”] Ndi atate angati ali pano? Ndani mmodzi wa inu dzina lake liri “Atate”? Ndi ana angati ali pano? Ndi anthu angati ali pano? Mukuwona? Chabwino, ndani mmodzi wa inu dzina lake liri “Atate,” “Mwana,” kapena “Munthu”? Mukuwona?

155 Monga mkazi ananena nthawi imodzi, iye anati, “M’bale Branham, ‘Mzimu Woyera’ ndi dzina. Iwo ndi Munthu.”

156 Ine ndinati, “Inde, bwana. Ine ndine munthu, koma dzina langa siliri ‘Munthu.’ Ine ndine munthu, mwawona. Dzina langa ndi William Branham; koma ine ndine munthu.”

Mzimu Woyera uli Munthu. Ndicho chomwe Iwo uli. Ilo siliri dzina: ilo liri udindo wa Munthu wa Mulungu. Mukuwona? Ilo liri udindo ku umunthu wa Mulungu, chomwe Iye ali. Tsopano—tsopano ngati . . .

157 Iye anati, “Pitani inu chotero, ndipo mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, Mzimu Woyera.” Osati “mu dzina la Atate, dzina la Mwana, dzina la Mzimu Woyera.” Kapena, osati “mu *mayina* a Atate, ndi a Mwana, ndi a Mzimu Woyera,” koma, “Mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ndipo ngati “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” siziri dzina, ndiye nanga bwanji izo?

158 Titi ngati liri “dzina,” chabwino, limodzi liti? Inu mukufuna kulitcha limodzi la iwo dzina, dzina lake ndi liti? Ngati inu mukufuna kutcha udindo dzina, ndiye dzina lake liti, ndi udindo wuti womwe inu mukufuna kubatiza nawo “Atate” kapena “Mwana”? Ndi limodzi, mwawona.

Tsopano ife tisegule cha apa, ndipo ndilo bukhu lotsiriza la Mateyu.

159 Monga ine nthawizonse ndafotokozera izo. Ngati inu muwerenga nkhani ya chikondi, ndipo itanena, “Yohane ndi Mariya anakhala moyo wokondwa kuyambira pamenepo.” Mwawona, ziri chifukwa inu simuli—inu simukudziwa yemwe

Yohane ndi Mariya ali. Bwererani koyamba kwa nkhani yanu, mukapeze yemwe Yohane ndi Mariya ali. Mukuwona?

¹⁶⁰ Tsopano ndicho chomwe inu mukuchita apa mu Mateyu. Inu mukuwerenga gawo lotsiriza la izo lokha. Bwererani koyamba kwa Mateyu ndipo mukawerenge chomwe nkhaniyo ili. Uwu ndi mutu wotsiriza wa Mateyu, ndi ndime zotsiriza.

¹⁶¹ Monga inu mutatenga bukhu, ndi kunena, “Yohane ndi Mariya anakhala moyo wokondwa kuyambira pamenepo. Ameneyo anali Yohane Yonasi ndi—ndi Mariya *Wakuti-ndi wakuti*? Uyo anali. . . ? Ayi, ameneyo anali Yohane. . . ? Ameneyo anali Yohane Henere ndipo uyo anali *Wakuti-ndi-wakuti*? Uyu ndi Yohane *Winawake* ndipo *Wakuti-ndi-wakuti*?” Ayi, inu simukudziwabe, inu mukuwona. Chinthu chokhacho choti muchite, kuti mukhale wotsimikiza, ndicho kubwerera mu bukhu ndi kukawerenga izo. Mukuwona, inu simungakhoze kutenga kachidutswa *apa*. Inu muyenera kuyika chinthu chonse pamodzi, kuti mupange chithunzi.

¹⁶² Tsopano bwererani ku Mateyu, mutu woyamba. Ndipo iyo ikupita ndi kupereka mibadwo, kumabwera mmusi mwa mutu woyamba. Ndiye iyo ikufika ku ndime ya 18, ndipo ikuti, “Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali chotere.” Kodi nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁶³ Tsopano ine ndikufuna ndikufunsi inu chinachake. Tsopano mverani kachiwiri. Inu, inu muchitchule icho. [M’bale Branham aloza kwa chirichonse cha zinthu zitatu monga zofotokozera—Mkonzi.] *Uyu* ndi ndani? Mulungu. . . [Osonkhana, “Atate.”] Mulungu. . . [“Mwana.”] Mulungu. . . [“Mzimu Woyera.”] Tsopano mmodzi *uyu* ndi ndani? [“Atate.”] Mmodzi *uyu* ndi ndani? [“Mzimu Woyera.”] Mmodzi *uyu* ndi ndani? [“Mwana.”] Mwana. Chabwino. Tsopano ife tamvetsa izo tsopano. Tsopano inu munati *uyu* anali ndani; Mulungu *nda*? [“Mzimu Woyera.”] Mzimu Woyera. Chabwino. Tsopano, chabwino.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali kotere: Pamene. . . amayi ake Mariya anapalidwa ubwenzi kwa Yosefe, iwo asanakhalire pamodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa. . .

¹⁶⁴ [Osonkhana ati, “Mzimu Woyera.”—Mkonzi.] Tsopano, ine ndimayesa inu munati Mulungu anali Atate Ake. Tsopano pali chinachake cholakwika apa; Iye sangakhoze kukhala nawo Atate awiri. Inu mukudziwa zimenezo. Mwawona? Tsopano apo pali chinachake cholakwika. Tsopano mmodzi wuti wa Amuna awa, ngati iwo ali Anthu atatu, ndi mmodzi wuti wa Iwo ali Atate Wake? Baibulo limanena apa, momveka, “Iye anapezeka naye mwana wa Mzimu Woyera,” Mulungu Atate analibe chochita nacho icho. Ndipo Yesu anati Mulungu anali Atate Ake, ndipo ife tikudziwa Mulungu anali Atate Ake. Ndiye, Iye anali nawo

atate awiri; tsopano Iye ali wapathengo, motsimikiza kokwanira. Tsopano onani pamene inu mwadzipezera nokha? Tsopano:

Ndiye Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama . . . mopanda kufuna kumunyazitsa iye poyera, analinga kuti amusiye iye mwamseri.

Koma pamene iye ankaganizira pa zinthu izi, . . .

165 Kumbukirani, iye anali munthu wabwino, tsopano. Ndipo dzanja la Ambuye liri dzanja monga tsopano; iwo omwe anakonzedweratu adzaligwira ilo. Mukuwona?

Koma pamene iye ankaganizira pa zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto, . . .

Kodi inu mukutsatira mu Baibulo lanu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino.

. . . kunena, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope ayi. . . dzitengere kwa iwe Mariya mkazi wako: pakuti icho chimene . . . cholandiridwa mwa iye chiri cha . . .

166 “Mulungu Atate”? Kodi ine ndinawerenga mophophonyetsa izo? [Osonkhana ati, “Inde.”—Mkonzi.] Ndithudi ndinachita. “Icho chimene chiri cholandiridwa mwa iye,” chiribe chochita naye Mulungu Atate, ndi “Mzimu Woyera.” Ndipo tsopano ife tikudziwa kuti Mulungu anali Atate Ake. Kodi nkulondola uko? [“Ameni.”] Kotero nchiyani icho? Mzimu Woyera uli Mzimu wa Mulungu, ndithudi. Tsopano inu mwamvetsa izo. Mwawona?

167 Mulungu Atate ndi Mzimu Woyera ali Munthu yemweyo, kapena Iye anali ndi abambo awiri. Ndiyano chiyani—ndi munthu wa mtundu wanji yemwe inu mumampembedza? Inu muli ndi Mulungu wa mtundu wanji tsopano? Mukuwona? Mukuwona? Mulungu Mzimu Woyera, ndi Mulungu Atate, uli Mzimu womwewomwewo.

Ndipo iye adzabala mwana, . . . (Munthu uyu apa) . . . ndipo iwe udzamutcha dzina lake . . .

Chiyani? [Osonkhana ati, “YESU.”—Mkonzi.] “Dzina Lake!” [“YESU.”] Tsopano kumbukirani.

. . . dzina lake YESU: pakuti iye adzapulumutsa anthu ake kwa . . . ku machimo awo.

Tsopano ichi chonse chinachitidwa, kuti chikakwaniritsidwe chomwe chinanenedwa ndi Ambuye mwa mneneri, kwa yemwe Mawu amafikirako, kunena,

Tawonani, namwali adzakhala naye mwana, ndipo adzabala mwana, ndipo iwo . . . kumutcha dzina lake Emanuele, lomwe likumasuliridwa, Mulungu ndi ife.

168 Dzina la Mulungu ndi chiyani? Dzina lake ndani Atate, Mwana, Mzimu Woyera? [Osonkhana ati, “YESU.”—Mkonzi.] Baibulo linati “YESU” linali Dzina Lake.

Ndiye mzanga apa kuyesa kutsutsana nacho icho kamodzi, kuno mu kachisi, anati, “M’bale Branham waphiriphitha kuchoka mwa izo zonse, koma iye sachitha chimodzi ichi.” Anati, “Apa izo zikuwonetsa anthu atatu osiyana, chimodzimodzi, mwangwiro.” Anati, “Mateyu, mutu wa 3! *Apa* panali Yohane atayima, kulalikirira; *apa* panabwera Mwana, akuyenda kutha abatizidwe. Iye analowa mmadzi, anabatizidwa ndi Yohane; anapita mmbuyo potuluka mmadzi. Ndipo, ‘Tawonani,’ anati, ‘miyamba inatseguka kwa Iye.’ Ndipo anati, ‘Kutsika kuchokera Kumwamba kunabwera Mzimu Woyera, monga nkunda ikutsika. Ndipo Liwu kuchokera Kumwamba, likunena, ‘Uyu ndiye Mwana Wanga wokonedwa, mwa yemwe. . .’” Anthu atatu osiyana, pa nthawi imodzi kumene.” O, mai!

¹⁶⁹ Eya. Izo zimangopita kuti zisonyeze kuti anthu opanda ubatizo, ndipo osayitanidwa ku udindo wa—wa m—mtumiki, alibe ntchito kuti akhale mu guwa. Uko nkulondola.

Ine—ine—ine ndikhoza kumutenga munthu ameneyo, tsopano, mwa kuthandiza kwa Mulungu, ndi kuwamanga iwo mu mfundo yotero mwakuti zikhoza kupangitsa mutu wawo kusambira. Penyani, ine sindikusamala chiyani. . .

Osati, ine sindikutanthawuza “ine.” Izo sizikumveka molondola. Mundikhululukire ine. Ine sindimatanthawuza izo, Ambuye. Ine sindimatero, tsopano. Ine ndinamverera Iye akunditsutsa ine pa chimenecho, mwawona, kotero ine sindinatanthawuze kunena icho mwanjira iyo. Ndiri—ndiri kupepesa. Ine ndikukhulupirira kuti Mzimu Woyera ukanakhoza kuwulula kwa munthu ameneyo chinsinsi china. Izo zikumveka bwinoko.

¹⁷⁰ Ziri monga ngati kukunga ching’wenyeng’wenye, pamene iwe uchita chinachake cholakwika. Ndipo iwe umakhoza kudziwa icho, monga Mkristu, iwe unanena chinachake cholakwika. Iye sanachikonde icho. Mwawona, icho chinali kundiyika ine mmenemo. Mukuwona? Ine sindiri mu chithunzi, nkomwe. Ndiri chabe. . . sindifuna ngakhale kukhala inemwini kapena kanthu. Iye basi, kumulola Iye kuchita ntchitoyo. Iye amachita kuwombako. Lipenga limakhala duu; liwu paseri pa ilo, ndilo lomwe limapereka phokoso.

¹⁷¹ Tsopano, penyani apa. Munthuyo anamasulira molakwika Mawu. Mwawona, Izo. . . Kumbukirani, “Ziri zobisika kwa maso a anzeru ndi aluntha; kuwululidwa kwa makanda.”

Tsopano, *apa* pali Munthu mmodziyo, Yesu Khristu, akuyima pa dziko lapansi. Tsopano, miyamba; chifukwa, kuli milengalenga mmwambamo. Tsopano yang’anani, “Ndipo Yohane anachitira umboni. . .”

¹⁷² Tsopano munthu ameneyo ayenera kunena kuti, “*Apa* pali Mulungu Atate; ndipo *apa* pali Mulungu Mzimu Woyera, wonga

nkhunda; ndipo *apa* pali Mulungu Mwana; kupanga anthu atatu.” Ndizo zolakwika.

173 Yohane, atayima kumbuyo *apa*, anadziwa *uyu* anali Mwanawankhosa. Yohane anati, “Ine ndikuchitira umboni, kuwona Mzimu wa Mulungu monga Mwanawankhosa. . .” Apo pali Mulungu Mzimu, monga nkhunda, ine ndikutanthawuza. Tsopano apo pali chinthu chomwecho ine ndinanena usiku wina, inu mukuwona; mmalo mwa mazana asanu ndi awiri, zi- . . . Mukuwona? Mzimu wa Mulungu! Uyu anali Mwanawankhosa *apa*. Ndipo Mzimu wa Mulungu, Nkhunda, anali Mulungu. “Mzimu wa Mulungu ukutsika kuchokera Kumwamba. Ndipo Liwu kuchokera Kumwamba, likunena, ‘Uyu ndiye Mwana Wanga wokonedwa, mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo.’”

“Mphamvu zonse Kumwamba ndi dziko lapansi zapatsidwa mu dzanja Langa.” Mukuwona? Mukuwona? Mukuwona? Ndiye Iye. Tsopano Dzina Lake linali chiyani? [Osonkhana ati, “YESU.”—Mkonzi.] Ndithudi. Mwawona?

174 Koteri, kunena za ganizo la utatu, lokhala Amulungu atatu osiyana, icho ndi chikunja! Izo sizinaphunzitsidwe nkomwe mu Baibulo. Izo sizinaphunzitsidwe nkomwe mu Uthenga wa mkango, koma izo zinatengedwa mwa wotsatira, yemwe anali wotsutsakhristu. Mumufunse aliyense inu mungafune kumufunsa, wazaumulungu aliyense. Izo sizinabwere konse, kokha kupyolera mu chiphunzitso cha Achinikolai. Apo pali chifukwa chake icho chinatuluka ndi Marteni Lutera; ndicho chifukwa chake icho chinapirira ndi Joni Wesile; ndipo chinatsanulira mpaka mmusi kwa Achipentekoste.

175 Mu tsiku limene Chipentekoste chinatuluka, iwo anatenga gulu la “Yesu Yekha.” Tsopano, izo nzolakwika, aponso. Yesu angakhoze bwanji kukhala Atate wa Mwini Wake? Mukuwona? Koteri icho chikukankhira chimenecho kunja

176 Koma apo pakuyenera kukhala kuti nthawi ya mphungu ibwere. Mukuwona? Ndiyo nthawi Iti iwongole zinsinsi zonse izo. Mukuwona?

177 “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” ndi maudindo a Ambuye Yesu Khristu. Yang’anani, onse atatu awo! Mateyu anati, “Atate, Mwana, Mzimu Woyera?” Petro anati “Ambuye Yesu Khristu.” Atate ndi ndani? “Ambuye anati kwa Ambuye wanga, ‘Khala Iwe pa dzanja Langa lamanja.’” Kodi nkulondola uko? Atate; Mwana, Yesu; Mzimu Woyera, Logosi yomwe inatuluka kuchokera kwa Mulungu. “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” ali mwamtheradi mawudindo atatu a Munthu wa Mulungu kuwonetseredwa mu—mu—mu njira zitatu zosiyana, kapena malingaliro atatu a Iyemwini.

178 Ndipo kuzipanga izo kumveka, kwa winawake yemwe sakanamvetisa, ziri ngati udindo utatu wa Mulungu yemweyo.

Makamaka, ndi malingaliro atatu a Mulungu yemweyo. Mulungu akuchita mu utatu, wosiyana; pansi pa Utate, pansi pa Umwana, pansi pa nyengo ya Mzimu Woyera. Mulungu ali wangwiro mu utatu. Inu mukukumbira nambala ya wotsutsakhristu, kanayi? Mwawona? Mulungu, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ali mwamtheradi “Ambuye Yesu Khristu.”

¹⁷⁹ Pamene inu mubatiza, Dzina la “Yesu” lokha, uko nkulakwitsa. Basi, “Ndikubatiza iwe mu Dzina la Yesu,” izo mwamtheradi nzolakwika. Ine ndikudziwana nawo Ayesu ambiri. Bwanji, mayiko Achilatini ali odzaza ndi iwo, Ayesu.

¹⁸⁰ Koma uyu ali “Ambuye Yesu Khristu,” zikufotokoza chimodzimodzi Yemwe Iye ali.

¹⁸¹ Alipo a Branham ambiri, ngati inu mukufuna kulankhula za ine pandekha, koma ndiri—ndiri William Marrion Branham mmodzi. Uyo—ndiye ine. Koma alipo ambiri ma William Branham ena, ndi ena otero, kozungulira.

¹⁸² Koma uku kuli mwatchutchutchu kuyitana Munthu mmodzi, Ambuye Yesu Khristu, mwawona, Mmodzi wodzozedwa. Alipo Mmodzi yekha wa iwo. Tsopano, uko nkulondola.

Kotero ngati pali kupitiriza kulikonse kwa izo, inu mulembe kalata kapena chinachake, kapena—kapena nthawi yina pamene ndiri pa mafunso ena. Ine ndikufuna kuyesa kutenga ili, kotero ine ndikhoza kuwona ngati ife tingakhoze kutenga ena a anthu odwala awa omwe akuvutika, kuti apemphereredwe.

184. M’bale Branham, ngati funso ili siliri—siliri loyenera, silikuyenera umu... musaliyankhe. (Ndiwo ubwino. Ine ndikuyamikira izo.) Ana ati—ndi ana ati amene akupita mu Mkwatulo, ngati pali aliwonse aang’ono? Zikomo.

Iwo sanalembe dzina ayi. Tsopano, ngati inu simutero, ilo siliri lofunikira.

¹⁸³ Koma, penyani. Pamene Mulungu ayika dzina pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko asanayikidwe, palibe kanthu mu dziko kangakhoze kulifutapo ilo, chifukwa ilo linalembedwa ndi inki ya Magazi a Khristu. Angakhale wamkulu *choncho*, wamkulu *chonchi*, kapena wamkulu *choncho*, kapena chirichonse chimene icho chingakhale, izo zimapita mofanana basi. Mukuwona? Ana onse, Mpingo wonse, chirichonse chomwe chiripo, chiri... Mulungu, mwa kudziwiratu Kwake.

¹⁸⁴ Tsopano, ife sitikudziwa. Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mungatsimikizire kuti inu muli mmenemo?” Ayi, bwana. Ine sindingakhoze kutsimikizira izo. Mulungu akanakhoza kundigwiritsa ine kwa chida cha chinachake, ndi kukugwiritsani inu mwanjira yomweyo. Koma ine ndikukhulupirira, ndipo mwa chikhulupiriro, ine ndapulumutsidwa. Osati mwa chidziwitso ine

ndapulumsidwa; mwa chikhulupiriro! Ndimomomwe inu mwapulumsidwira. Ndimomomwe ife tonse tapulumsidwira.

¹⁸⁵ Koma, kumbukirani, Mulungu ali wopandamalire. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Wopandamalire! Chabwino, pokhala wopandamalire, icho chikumupangitsa Iye...Ndipo, ndiye, Iye ali wodziwazonse. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [“Ameni.”] *Kudziwazonse* kumatanthawuza “Iye amadziwa zinthu zonse.” Iye sangakhoze kukhala—Iye sangakhoze kukhala wodziwazonse popanda kukhala wopandamalire. Mwawona, apo panalibe kanthu koma komwe Iye ankakadziwa. Iye ankadziwa tongole aliyense yemwe ati adzakhale konse pa dziko lapansi, ndi kuchuluka kwa nthawi yomwe iye ati adzaphethire maso ake, kuchuluka kwa phula lomwe iye akanadzapanga, kuchuluka kwa lomwe onse ati adzapange pamodzi. Iye anadziwa kupuma kulikonse komwe inu mukanadzapuma, ndi kuya komwe iko kukanadzalowera mu phapo lanu. Uko nkupandamalire.

¹⁸⁶ Tsopano, ngati Iye ali wopandamalire, icho chikumupanga Iye kukhala wodziwazonse. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo ngati Iye ali wodziwazonse, icho chikumupanga Iye kukhala wopezekapaliponse, chifukwa Iye amadziwa chimodzimodzi basi miniti, ora, nthawi, mpaka gawo la mphindi la makumi asanu ndi zisanu pa zikwi ya mphindi, mpaka pamene izo ziti zikachitike. Mwaona? Mwapeza lingaliro tsopano? [“Ameni.”] Ndiye, Iye amadziwa zinthu zonse. Ndipo ndicho chifukwa chake Iye ali nayo mphamvu yonse, amadziwa zinthu zonse, ndipo akhoza kuchita zinthu zonse.

¹⁸⁷ Tsopano tiyeni tiwone. Tsopano, “Ndipo ana onse omwe Mulungu...Mmodzi aliyense yemwe Mulungu...Pamene iwo...” Tsopano, kumbukirani, pamene anali Yesu...Baibulo linati...

¹⁸⁸ Tsopano ife tikudziwa kuti Yesu anaphedwa pafupi A.D. 30. Ndi kulondola uko? Pafupi, panali pafupi pakati pa chaka, ine ndikuganiza, A.D. 30.

¹⁸⁹ Tsopano, koma Baibulo linanena kuti Iye anaphedwa dziko lisanalengedwe konse. Ndipo dzina lanu, pamene Bukhu la Mwanawankhosa...Pamene Mwanawankhosa anaphedwa, kuti awombole Bukhu ili...Apa pali chinthu chachikulu tsopano. Icho chikhoza kuyambitsa kukondoweza. Penyani. Pamene p—pamene p—pamene Mwanawankhosa...Tsopano kumbukirani, Baibulo linati Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa linalembedwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Ndipo dzina lanu linayikidwamo, linali mu Bukhu limenelo pamene Mwanawankhosa ankaphedwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe, kuti awombole dzina lirilonse lomwe linalembedwa mu Bukhu limenelo. Mukuwona? Mwamvetsa izo tsopano?

¹⁹⁰ Mwawona, palibe kanthu kamene kachoka mu dongosolo. Izo zikugwira ntchito chimodzimodzi basi monga chosunga nthawi chachikulu cha Mulungu, mwawona, monga koloko ikusuntha chozungulira molondola. Dzina lanu linayikidwa mmenemo maziko a dziko asanakhazikitsidwe, pamene Mwanawankhosa anaphedwa kuti awombole chomwe chinali mu Bukhu limenelo. Ndipo tsopano Iye akubwera patsogolo ndipo akutenga Bukhu limenelo, kuti atenge chiwombolo Chake.

Ine sindikufuna kuyamba apo; ife sitingayankhe funso lina nkomwe lero. Chabwino. Funso:

185. Kodi gehena, ndi nyanja yomwe ikuyaka nawo moto ndi miyala ya sulfure, ndi zofanana?

¹⁹¹ Ayi. Gehena, kumasulira mu Baibulo, ine ndikukhulupirira... Tsopano, pano pali masakolala akhala pano, ndipo ine ndikufuna kulemekeza izo. M'bale wathu Iverson wakhala apa, ndi M'bale Vayle, ndi ambiri a abale awa omwe ali azaumulungu enieni. Mawu omasuliridwa, *hade*, amatanthawuza "manda." Ndi nkulondola uko? Mawu a Chigriki a manda. Koma Nyanja ya Moto ili chinachakenso. Chifukwa, uko mu Chivumbulutso, "Zonse, hade ndi zonse, zinaponyedwa mu Nyanja ya Moto." Mukuwona? Chabwino. Tsopano tiyeni tiwone.

186. Ngati sichoncho, kodi Nyanja ya Moto, ndi gehena, Nzamuyaya?

¹⁹² Ayi, bwana. Ayi, bwana. Chirichonse chimene chinalengedwa sichiri Chamuyaya. Ayi. Chirichonse chomwe chinalengedwa... Ndicho chifukwa chake sipangakhale gehena Wamuyaya. Ngati aliyense akuwuzani inu izo kuti inu mukawotchedwa mu gehena Wamuyaya, ine ndikufuna Lemba la izo. Mwawona? Palibe chinthu chotero ngati izo.

¹⁹³ Gehena analengedwera Mdierekezi ndi angelo ake, kwa wotsutsakhristu ndi anthu ake; ameneyo anali Mdierekezi, Mdierekezi mu thupi. Iyo inalengedwera zimenezo, kuti awononge. Ndipo chirichonse chomwe chinali... Chirichonse...

¹⁹⁴ Pali chinthu chimodzi chokha, nkomwe, kuchokera mu chirichonse chomwe chiripo, dziko lonse ndi china chirichonse, pali chinthu chimodzi chokha Chamuyaya, ndipo ndicho Mulungu. Kusanakhale atomu, kapena nyese kapena kusanakhale ngakhale kuwala kwa mdziko, nyese kapena chirichonse, Iye anali Mulungu. Iye ndi Mlengi.

¹⁹⁵ Ndipo ndiyo njira yokhayo inu mungakhazere kukhala Wamuyaya, ndiyo kulandira Moyo Wamuyaya. Mawu a Chigriki aja pamenepo, ine ndikuganiza, ndi *Zoe*. Si kulondola uko? *Zoe*. *Zoe*. Ndiyeno, uwo—Moyo uwo, Mulungu amawugawira kwa inu. Monga atate, atate anu, amagawira moyo wake kwa

inu, kupyolera mu l—lumbiriro la chikwati ndi amayi; ndi iwo, potero, amagawira, c—chimwemwe cha kugawira, (ndimvetseni ine) za kugawira moyo kwa mwana. Ndipo ndiyo njira yomwe Mulungu amachitira, chimwemwe mu kugawira Moyo Wake kwa mwana. Mukuwona? Ndiyeno inu mumakhala gawo la Iye, lomwe liri Zoe, Moyo Womwe wa Mulungu. “Ine ndipereka kwa iwo Moyo Wamuyaya.”

¹⁹⁶ “Kuwadzutsa iwo, tsiku lotsiriza.” Ndicho chinthu chokhacho chomwe—chomwe... Inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo Moyo Wamuyaya uwo umalidziwa thupi Lake, ndipo ilo liyenera kutulukira. Kuti ilo likhoze... Ndi kosatheka kuti ilo ligone pamenepo. Pamene Mzimu wa Khristu unafungatira pa thupi, Mzimu wa Mulungu pa Khristu, pa tsiku lalikulu lija, ilo linkadziwa kuti ilo lidzawuka kachiwiri; kotero ali oyeru mu thupi lawo.

¹⁹⁷ Tsopano kumbukirani. Yesu, pamene Iye anafa, Iye anapita ku gehena. Chifukwa, Iye anayenera kupita kumeneko; Iye anali chotchinga-tchimo. “Ndipo Iye analalikira kwa miyoyo yomwe inali mu gehena, yomwe siyinalape mu kupirira-kotalika, masiku a Nowa.” Nkulondola uko? Iye anapita ku gehena ndi kukalalikira kwa miyoyo, miyoyo yolekanitsidwa kwa Mulungu. *Imfa* imatanthawuza “kulekanitsa.” Ndipo iwo anali atalekanitsidwa kwa Mulungu, sakanakhoza kudzabwereranso nkomwe. Ndipo Yesu anapita kukachitira umboni kuti Iye anali Mmodzi yemwe analankhulidwa, m—Mbewu ya mkazi.

¹⁹⁸ Mbewu ya serpenti, mwawona chimene mbewu ya serpenti inachita? Wotsutsakhristu; akutsirizira mu imfa, kulekanitsa, kavalo wofiira. Mbewu ya mkazi, Moyo, ukuthera pa kavalo woyera, Yesu Khristu. Mukuwona? Nchiyani icho? Chimodzi kutsutsa chimzake; mbewu ya serpenti kutsutsa Mbewu ya mkazi. Mwamvetsa izo tsopano? O, ife tikanakhoza kukhala kanthawi pang’ono pa izo! Kodi sichikanakhala chabwino icho? Koma tiyeni tikhale ndi ili.

187. M’bale Branham, kodi wokwera pa kavalo woyamba, Chisindikizo Choyamba, akukwaniritsa Atesalonika Wachiwiri, “vumbulutso la munthu wa tchimo”?

¹⁹⁹ Inde. Uko nkulondola. Ndi momwemo. Ilo ndi lophweka. Ndi momwemo. Ameneyo ndi munthu wa tchimo. Munthu yemweyo akupitirira basi, mu masiteji, akukwerabe mpaka iye atafika pa kavalo wotumbululuka yemwe akutchedwa “Imfa.” Khristu akubwera mpaka mmusi kupyola mu, kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, kwa kavalo woyera ndipo ndiwo Moyo uwo, inu mukuwona.

188. Chinachitika nchiyani kwa okhulupirira obadwaka-chiwiri omwe ali mu zipembedzo zosiyana koma osati mwa Mkwatibwi wa Khristu? Chiti chichitike nchiyani kwa iwo?

²⁰⁰ Chabwino, ine ndikuganiza ife tinafotokoza izo, kanthawi kapitako. Mukuwona? Iwo akupita mu Chisawutso. Iwo akuphedwera mu Chisawutso. Kutulukira potsiriza, zitatha Zakachikwi, kwa chiweruzo chawo. Mukuwona? Chifukwa, Baibulo linanena kuti amoyo ena onse...“Akufa onse sanakhalenso moyo mpaka zaka chikwi zitatha.” Ndiye kunali chiwukitsiro, ndiyeno anatulukira onse, olungama ndi osalungama, ndipo anaweruzidwa ndi Khristu ndi Mkwatibwi. Iye anabwera ku dziko lapansi ndi zikwi khumi kuphatikiza zikwi khumi za oyera Ake. Nkulondola uko? Mkwatibwi Wake.

²⁰¹ Chiweruzo chinakhazikitsidwa. Mabuku anateguledwa. Mabuku anateguledwa. Ndipo Bukhu lina linateguledwa, lomwe linali Bukhu la Moyo. Iye analekanitsa, kuchokera pamenepo, mbuzi kwa nkhusa. Ndi kulondola uko? Izo zinalibe chochita naye Mkwatibwi. Iye anali kuyima pomwepo mu chiweruzo, ndi Mfumukazi yake...Mfumukazi ndi Mfumu, palimodzi. “Iye anabwera ndi oyera Ake; zikwi khumi kuphatikiza zikwi zinatumikiza kwa Iye,” mkazi Wake. Ndiye chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndiyeno nkhusa zinalekanitsidwa kwa mbuzi. Mukukumbukira usiku wina, ine ndikubweretsa kusinkhasinkha kwakung’ono kuja, kotero inu mukanakhoza kumvetsa izo, kusinkhasinkha kwa wolishang’ombe? Mukuwona? Ndi zimenezotu.

²⁰² Ayi, iwo, ndicho iwo, m—m—mpingo, anthu omwe ali mu zipembedzo, omwe ali—ali Akhristu enieni, omwe alandira Uthenga ndipo iwo sadzawuwona konse Iwo. Iwo sudzalalikidwa kwa iwo. Ndipo awa a mu magulu osanganikirana, omwe Iwo ukulalikidwako, Iwo udzadzutsa pamwamba pa mitu yawo pomwe, pokha ngati dzina lawo linali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhusa. Eya. Koma iwo adzakhala anthu abwino.

²⁰³ Ndipo iwo adzawukitsidwa kachiwiri ndi kupatsidwa mulandu, ndi kuweruzidwa ndi gulu lomwelo limene linalalikira kwa iwo. “Kodi inu simukudziwa oyera adzaweruzo dziko lapansi?” Iwo adzalalikiridwa, mwawona. Iwo adzalalikiridwa, ndi anthu omwewo amene anachitira umboni kwa iwo za Uthenga, kuti “Tulukani kwa izo!” Mukuwona? Ine ndikuyembekeza izo zikufotokoza ilo. Ine ndiri nawo ochuluka apa, omwe... .

189. M’bale Branham, kodi mngelo wachisanu ndi chiwiri, wokhala nawo mzimu wa Eliya, ndi munthu yemweyo monga Eliya wotumizidwa kwa Ayuda zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi pa nthawi ya zaka zitatu ndi theka utachitika Mkwatulo? Ena a ife tasokonezeka, mu izi.

²⁰⁴ Ayi. Iye sali yemweyo. Mwawona, ali anthu awiri osiyana. Elisha yemwe anabwera mu mawonekedwe a Eliya sanali Eliya. Ndipo mzimu wa Eliya womwe unabwera pa munthu wotchedwa

Yohane M'batizi sanali Eliya. Ndipo munthu wa mtumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, pa mapeto a M'badwo wa Laodikaya, sadzakhala Eliya weniweni. Iye adzakhala Wamitundu, kwa anthu ake.

²⁰⁵ Eliya adzakhala, kapena mzimu wa Eliya ndiye, kubwera mu...ndi kwa anthu pamenepo, iye adzakhala Myuda, mwawona, pakuti iwo akutumidwa kwa anthu awo omwe. Ndilo vumbulutso langa. Chifukwa ine...Za Tommy Osborn, pamene ife tinkalankhulana pa izo, nthawi ija, Tommy ndi ine, ine sindinkadziwa. Ine ndinali kungopempherera odwala.

²⁰⁶ Ndipo ine ndinabwera pamenepo, ndipo apo panali dona atabwera uko kuchokera ku Fort Wayne Gospel Tabernacle, misionare ku minda yakunja. Bere lake linali lalikulu *chonchi*, linali litangodyedwa ndi khansara. Ndipo iye anali pomwe apo mu nyumba yaying'ono komwe ife tinkakhala, kumtunda kuno mu msewu. Ndipo ine ndinamupempherera mlongo wokoneddwayo. Ndipo iye anachiritsidwa, ndipo anabwerera ku munda. Ndipo pamene...Iye anabwera kuchokera ku Afrika. Ndipo iye analita atasiya kabuku kakang'ono kumeneko, ka mamishoni.

²⁰⁷ Ine—ine ndinaganiza, “Chabwino, mamishonare ndi abwino.” Ndipo ine...Ine sindinkaganiza kwambiri za mamishonare. Ndipo kotero ine ndinaganiza, “Chabwino, iwo ali chabe udingo wa Mulungu kunjira uko. Kotero ndicho... Awa ndi malo anga pomwe pano, pa Eighth ndi Penn Street.” Kotero ine ndinali kumangopitiriza momwe ine ndikanakhoza kuchitira.

²⁰⁸ Koma tsiku limodzi, nditakhala mowerengera, ine ndinanyamula bukhu lija. Ndipo ilo linali ndi chithunzi cha—cha wa mtundu wa Chiniguro, bambo wakale wachikulire, ndipo iye anali nawo mkombero uwu wa tsitsi loyera. Ndipo mmusi munalembedwa monga *chonchi*, “Mzungu, mzungu, abambo ako anali kuti? Mwawona, ine ndiri tsopano wamkulu ndi wofowoka pa kukumbukira, ndipo ine sindimvetsa kwambiri bwino. Ngati ine ndikanamudziwa Yesu pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, ine ndikanamutengera Iye kwa anthu anga.” Chabwino, ine ndinaliwerenga ilo.

²⁰⁹ Ndipo chinachake chinangopitirira kunena, “Werenga ilo kachiwiri. Werenga ilo kachiwiri.” Ine ndinapitiriza kuliwerenga. O, inu mwakhala nazo nthawi zimenezo. “Kuliwerenga ilo mobwereza bwereza. Muli chinachake mkati umo.”

²¹⁰ Monga kumtunda uko ku Green's Mill, pamene ine ndinatuluka ku mphanga. Ine sindinkakhoza kumvetsa izo, momwe anthu amakhosera kulankhula nawo malirime ndi kufuwula, ndipo ndi Mzimu Woyera weniweni, ndipo nkukhalabe wotsutsakhristu. Kulankhula ndi malirime,

Malirime enieni a Mzimu Woyera ukulankhula, ndipo nkukhalabe mdierekezi. Uko nkulondola. Ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu. Inde, ndithudi. Ndiyeno zindikirani. . . pamene iwo anayima pamenepo.

²¹¹ Kotero, malirime sali umboni wa Mzimu Woyera. Iwo ali imodzi mwa mphatso za Mzimu Woyera. Mukuwona? Ndipo Mdierekezi akhoza kukopera chirichonse Iye ali nacho, machiritso Auzimu ndi china chirichonse.

Iye anati, “Ambiri adzabwera kwa Ine tsiku limenelo, ndi kunena, ‘Ambuye, kodi ine sindinaturutse ziwanda? Ine sindina. . .’” Uko nkulalikira Uthenga. “Kodi ine sindinachite ntchito zamphamvu mu Dzina Lanu, ndi zinthu zonse izi kumeneko?” Ine ndidzanena, ‘Chokani kwa Ine, inu akuchita kusayeruzika. Ine sindinakudziweni ngakhale inu.’”

²¹² Baibulo linanena, kuti, “Mvula imagwera pa olungama ndi osalungama, mofanana.” Ndipo chisoso chomwecho, chikuyima mu munda wa tirigu uko, chikhoza kukhala chokondwa ndi kufuwula, ndi madzi omwewo omwe anagwera pa iye, pamene zonsezo zimatimizidwa kwa mvula. “Koma mwa zipatso zawo inu mumawadziwa iwo.” Chisoso chaching’ono icho chikhoza kuyima uko, ndipo mokondwa basi ndi kufuwula monga iye angathere, basi wodzaza nayo mvula yomweyo yomwe tirigu ali.

²¹³ Ndi zimenezotu. Kotero iwo akhoza kufuwula, kulankhula ndi malirime, ndi kukopera chirichonse iwo akufuna kutero; mu tsiku limenelo, nkutchedwa, “Antchito za kusewuzika.”

²¹⁴ Monga ine ndinakuwuzirani inu, kanthawi kapitako, mverani ku chomwe ine nditi ndinene! Mverani mwatcheru. Penyani mmbuyo pansu, dziyeseni nokha ndi Mawu ndipo muwone pamene inu muli.

²¹⁵ Inu akazi omwe muli ndi tsitsi lalifupi, lisiyeni ilo likule. Inu mukuvala makabudula; avuleni amenewo. Muzichita ngati dona. Inu amuna omwe mukanasutabe ndudu, ndi kumathamangira ku zipinda za juga, siyani zimenezo. Ine sindikusamala kaya inu mukudzinenera mochuluka bwanji. Ngati inu mukugwirabe chipembedzo chimenecho, ndi kumanena, “*Ichi* ndi Iwo, ndipo *ichi* ndi Iwo,” kuli bwino inu musiye. Yang’anani mmbuyo pansu, ziyeseni izo ndi Mawu. Iye tikufika mpaka kunjja kwa . . .

²¹⁶ Iye tinayenera kumakhala pamwamba pa tsitsi lalifupi ndi zonse. M’badwo uno tsopano, ife tabwerera ku Chinachake tsopano, kuti Mulungu akuwulula zinsinsi zobisika, zomwe zinali zitayikidwa pa Bukhu maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Ndipo iwo amene anamvera mu zinthu zazing’ono izi, adzagwira Izo mu zinthu zina izi. Ngati iwo sanatero, Izo zizadutsa pamwamba pa mutu wawo, kutalikirana monga kummawa kuli kuchokera kumadzulo. Iwo adzango. . .

²¹⁷ Monga Gidioni, kupatula anthu ake. Kunali zikwi ndi zikwi. Mulungu anati, “Iwo achulukitsa. Apatule iwo kachiwiri.” Iye

anawapatsa iwo yesero lina. Ndipo, “Apatule iwo kachiwiri. Apatule iwo kachiwiri.” Ndipo mpaka mmusi, mpaka iye anali ndi pang’ono okwana mdzanja. Iye anati, “Ndilo gulu lomwe ine ndikulifuna kuti lichite ntchito.” Ndizo chimodzimidzi zomwe zinachitika.

²¹⁸ Akazi Achipentekoste (kupita mmbuyo ndi patsogolo) atakhala pamenepo, akumva ndi kudziwa, mwa Mawu, izo nzolakwika. Inu mukuganiza kuti iwo agwirizana nazo Izo? Ayi, bwana. Chaka chirichonse, pamene ine ndikudutsapo, pali ambiri a tsitsi lodulidwa kuposa omwe analipo pamene ine ndinayamba.

²¹⁹ Anati, “Kodi izo ziri ndi chochita chanji...Iwe uyenera kuti...” Winawake anati, “Bwanji, M’bale Branham, anthu amakutangani inu ngati mneneri.” Tsopano, ine sindikunena kuti ine ndinali mneneri. Palibe aliyense amandimva ine ndikunena choncho. Koma ine ndinena ichi, kuti ngati—ngati inu mumachita zimenezo, ngati inu mumatenga izo...Anati, “Bwanji inu simumawaphunzitsa anthu momwe angalandirire Mzimu Woyera, ndi momwe angapezere *izi*, ndi momwe angapezere mphatso zauzimu ndi kumathandizira mpingo?”

Ine ndingawaphunzitse bwanji iwo aljebula pamene iwo samvera nkomwe kwa ABC wawo? Uko nkulondola. Inu mumachita zinthu zazing’ono *izi*. Khalani apa pansi ndi kuzichotsapo izo, ndi kuyamba molondola. Amen. Chabwino.

²²⁰ Ine ndinali kulankhula za chiyani, mulimonse? Tiyeni tiwone. Ine sindimatanthawuza kuti ndichoke pa mutu uwo. Mundikhulukire ine, mwawona. Chabwino. “Ena a...ena a ife tiri osokonezeka. Kodi Eliya ndi yemweyo ndi...” Eya, u-nhu, ndiko kulondola.

Ayi. Eliya uyu yemwe ati adzabwere kwa Amitundu, adzakhala Wamitundu wodzozedwa nawo mzimu umenewo, chifukwa Mulungu ankagwiritsa ntchito mzimu womwewo kuti uwabweretsere anthu Ake kuchokera mu chisokonezo nthawi iliyonse. Ndipo iwo unatumikira cholinga Chake bwino, kotero Iye akuwubweretsanso iwo pansi kachiwiri. Chifukwa, mwawona...

Chifukwa, tsopano, ngati Iye ati agwiritse ntchito wopukutidwa-wapamwamba, wophunzira, ndiwo mtundu womwe iwo ukanawugwira.

²²¹ Iye akubweretsa munthu yemwe sadziwa nkomwe ABC wake, ndipo sangakhoze kutchula mawu ake molondola, ndi chirichonse monga choncho; chinachake chakale cha kuchipululu kutsidya uko kwina wake, ndi kubweretsamo Iwo ndi kukankhira mmusi kumene kwa anthu a malingaliro-ophweka awo. [M’bale Branham akhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] Ndipo iwo amachitenga Icho, monga

choncho. Iwo amachitenga Icho, mwawona. Ngati Iwo abwera, ndi kolala . . .

²²² Monga Paulo anati, “Ine sindinabwere kwa inu ndi kupukuta kwa maphunziro, koma ine ndabwera kwa inu mu Mphamvu ya chiwukitsiro.” Icho chinamutengera Mulungu zaka zitatu ndi theka, kumusi mu Arabia uko, kukawachotsamo iwo mwa iye, maphunziro ake. Chinatenga—chinamutengera Iye zaka makumi anayi kuti akawachotse iwo mwa Mose. Mukuwona? Kotero ndi zimenezotu. Ndizo . . .

Ine sindikunena kuti Mulungu sati . . . Ine sindikuthandizira umbuli tsopano, koma ine—ine ndikuyesa kukuwuzani inu kuti sizimatengera . . . Maphunziro sati . . .

²²³ Nzeru za dziko lino ziri zosiyana. Maphunziro akhala cholepheretsa chachikulu chomwe Uthenga unakhalapo nacho. Ngati ife tikanapanda kukhala nawo maphunziro, ife sibwezi tiri ndi maseminare akulu ndi zinthu zomwe ife tiri nazo tsopano. Akanakhala anthu, a malingaliro—ophweka, omwe akanamvera kwa Mawu. Koma iwo ali opukutidwa chotero ndi osokonezedwa, ndi omangika kumeneko, ngakhale, mabungwe amenewo, mpaka kuti iwo apitirira kukhala nawo iwo. Ndizo zonse. Iwo akutengera mzimu umenewo. Kodi inu munayamba mwamutengapo mkazi wabwino, kumukwatitsa kwa mwamuna wachikhalidwe chonyansa? Mwamuna wachikhalidwe chonyansayo kapena amakhala m—mwamuna wabwino monga mkaziyo ali, kapena mkaziyo amakhala wachikhalidwe chonyansa monga iye ali. Mukuwona? Uko nkulondola.

²²⁴ Ndicho chifukwa chake Iye anati, “Tulukani pakati pa iwo, pamene Ine ndikukonzekera kuti nditenge Mkwatulo umenewo.” Inu muyenera kukhala nacho chikhulupiriro cha mtundu wina chomwe chidzakutengeni inu kukuchotsani kuno.

190. Linali liti pangano, la Daniele 9:27, pamene linatsimikizidwira kwa sabata?

²²⁵ Theka limodzi la ilo linatsimikizidwira, pangano, pamene Yesu Khristu anali pa dziko lapansi akulalikira kwa Ayuda. Iye sanapite konse kwa Amitundu, nkomwe. Ndipo Iye anawawuza ophunzira Ake, “Musati mupite kwa Amitundu.” Ilo linali kwa Ayuda, okha. Mwawona? Ndipo Iye analalikira kwa zaka zitatu ndi theka. Ndilo theka la sabata la makumi asanu ndi awiri, tsopano, monga Daniele anati Iye akanadzachita.

²²⁶ Tsopano kumbukirani, Iye anali wotsimikiziridwira mokhazikika kwa Myuda. Koma maso awo anachititsidwa khungu, kuti alowetsemo kadanga aka ka Wamitundu. Kodi inu simungakhoze kuwona dongosolo lonse? Mukuwona? Ndipo Iye anadzitsimikizira Yekha, mneneri, anachita chimodzimidzi basi chomwe mneneri akanachita, anawawonetsa iwo chizindikiro cha mneneri. “Chimene, Mawu anu omwe anati, ‘Ngati munthu

anena kuti ali wauzimu, kapena mneneri, yang'anani zomwe iye anena; ndipo ngati izo zifika pochitika, kumangopitirirabe kuchitika, zomwe iye ananena, mopitirira.' ”

²²⁷ Monga, inu muyang'ane mu Baibulo, ilo linati, “Gogodani, icho chidzatsegulidwa; funani, kupeza; pemphani, chipatsidwa.” Tsopano, ngati inu muti muzindikire, ndi “agogoda.” Kumangogogoda mowirikiza. [M'bale Branham akuyamba kugogoda pa guwa nthawi makumi awiri ndi katatu—Mkonzi.] Kukhala pomwepo. Monga woweruza wosalungama, sakanamuyankha mkazi; iye anapitiriza kugogoda pa chitseko chake. Kunena, “Ine ndiri pa dzanja Lanu.” [M'bale Branham akusiya kugogoda.] Osati kufuna, kuti, “Ambuye, ine ndikufuna nditakhala nacho *ichi*. Ameni.” Sindizo izo. Khalanibe pamenepo mpaka inu mutalandira icho. Inu mukudziwa kuti icho chibwera. Koteru, Iye analonjeza icho, koteru ingokhalani pomwepo mpaka inu mutagwira pa icho. Mukuwona?

Tsopano, tsopano, mu gawo lotsiriza, sabata la makumi asanu ndi awiri, gawo lotsiriza la ilo lidzakhala pa nthawi ya nyengo ya Chisawutso, utachitika Mkwatulo wa Mpingo. Ndiye apa pali zaka zitanu ndi theka apa, kuti ilo lidzatsimikizidwa kwa iwo kachiwiri ndi aneneri, mwawona. Mose ndi Eliya, Chivumbulutso 11. Tsopano tiyeni tiwone chomwe ili liri:

191. Ngati inu muli mmodzi wa osankhidwa Ake, kodi inu mudzapita mwa Mkwatibwi? (Inde. U-hu. Inde, bwana. Ilo ndi lophweka.)

192. M'bale Branham, kodi inu munatanthawuza kuti munene zikwi zisanu ndi ziwiri omwe anali asanagwadire bondo lawo kwa Baalimu, kapena mazana asanu ndi awiri?

²²⁸ Zikwi zisanu ndi ziwiri, ine ndinatanthawuza kuti ndinene. Mundikhululukire ine pa izo, mwawona. Basi. . . Kali chabe k—kachtidwe ka kulankhula. Ine ndinali chabe. . .

Monga, ndinanena kanthawi kapitako. Kodi inu munandizindikira ine nditayima apa, ine ndinati, “Ndipo—ndipo iwo akuchitira umboni, pomuwona Mwanawankhosa. . .”? Mwawona? Mwawona? Mwanawankhosa anali pa dziko lapansi. Mwawona? “Kuchitira umboni, powona Mzimu wa Mulungu ukubwera pa Mwanawankhosa.”

²²⁹ Tsopano, mmenemo, izo zinanenedwa, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa, mwa Yemwe Ine ndikukondwera bwino.” Inu mukuwona? Tsopano, izo zalembedwa mu mawonekedwe enieni a Chigriki, kuyika verebu patsogolo pa adiverebu. Koma inu zindikirani apa, izo zikhala makamaka izi. Tsopano ingotengani Mawu, mwawona. Baibulo limanena, mu kumasulira kwa Yakobo Woyera apa, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa, mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhala.” Koma, makamaka, ngati ife tikanati tinene izo monga ife timanenera

lero, “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo.” Inu mukanawatembenezira iwo mwina, mwawona. Mukuwona? “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhala.” Mukuwona? Tsopano, ife tikanakhoza kunena izo lero, “Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo.” Mwawona, mawu omwewo, kungowatembenezira iwo mwina. Mukuwona?

²³⁰ Tsopano, inde, ine ndimatanthawuza . . . Mundikhululukire ine, chonde. Ine . . . Ndipo—ndipo, abale, inu pa tepi kunja uko, ndi amzanga, mverani. I sindimatanthawuza kunena izo monga choncho. Ine—ine—ine ndine mtumiki wa Uthenga. Ine, nthawi zambiri monga ine ndalalikira zimenezo, ine ndimadziwa kuti awo anali zikwi zisanu ndi ziwiri. Ine ndinangopezeka ndikunena mazana asanu ndi awiri. Ine sindimatanthawuza chabe mazana asanu ndi awiri. Ine ndimatanthawuza, inu . . . Ine kungoti sindinawerenge izo kuchokera mu Lemba. Ichu chinangobwera ku malingaliro anga pamene ine ndinali kulankhula, ndipo ine ndinangonena mazana asanu ndi awiri mmalo mwa zikwi zisanu ndi ziwiri. Ine ndimapanga kulakwitsa kumeneko nthawi zonse. Ndine—ndine ndithudi mbuli, kotero inu mundikhululukire ine. Mukuwona? Ine sindimatanthawuza kuchita izo.

193. Kodi Mkwatibwi wa Khristu, ndi Thupi la Khristu, ali yemweyo?

²³¹ Inde, bwana! Mukuwona? Tsopano, apa, tsopano mwawona, ine sindikufuna kuyamba pa izo, chifukwa ine nditenga ul- . . . kulalikira ulaliki pa izo, mwawona. Koma ine sindichita izo. Koma ine ndikufuna ndikuwonetseni inu. Pamene Mulungu anamupatsa Adamu mkwatibwi wake, kuchokera ku mbali yake, iye anati, “Iye ali mnofu wa mnofu wanga, ndi fupa la fupa langa.” Nkulondola uko?

²³² Pamene Mulungu anamupatsa Khristu Mkwatibwi Wake, Mzimu unapereka thupi kwa Mkwatibwi, Iye anabowoledwa, analasidwa mu mbali pansu pa mtima Wake, ndipo madzi, Magazi, ndi Mzimu, zinatulukamo; izo zinakhala “mnofu wa mnofu Wake, ndi fupa la fula Lake.” Ife ndife mnofu ndi mafupa; Mkwatibwi adzakhala mnofu ndi mafupa a Khristu, chimodzimodzi. Iwo ali . . . Ameneyo ndi Mkwatibwi Wake.

194. Kodi Mkwatibwi wa Khristu adzakhala nawo . . . Kodi Mkwatibwi wa Khristu adzakhala nawo utumiki Mkwatulo usanachitike?

²³³ Zedi. Ndicho chimene chikuchitika pakali pano, mwawona, Mkwatibwi wa Khristu. Ndithudi. Ndi Uthenga wa ora, mwawona, Mkwatibwi wa Khristu. Zedi. Iye wapangidwa ndi atumwi, aneneri, aphunzitsi, alaliki, ndi abusa. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ameneyo

ndi Mkwatibwi wa Khristu. Zedi. Iye ali nawo utumiki, utumiki wawukulu, utumiki wa ora. Udzakhala wonyozeka kwambiri.

²³⁴ Tsopano kumbukirani. Ndi angati analipo pano, poyamba, pamene ine... Lamlungu latha, mwawona, mukukumbukira zomwe ine ndinalalikirapo? Kudzichepetsa. O, musati muyiwalezo. Ine ndiyima miniti, kuti ndichenjeze chimenecho kachiwiri. Kumbukirani, pamene Mulungu aneneratu chirichonse chachikulu choti chichitike, anthu amayang'ana kutali kwambiri, mwa nzeru zawo, mpaka iwo amaphonya chimene chikuchitika. Pamene Mulungu anena chirichonse kuti chiri chachikulu, dziko limaseka pa icho. "Gulu la mbuli ilo!" Uko nkulondola.

Koma pamene dziko lalikulu, ndi mpingo wawukulu wapamwamba, unena, "Mnyamata, ndicho chaulemerero!" Mulungu amati, "Gulu la mbuli!" Kotero, mwawona, inu muyenera kumayang'ana. Ine sindikutanthawuza izo zikhoza kukhala mwanjira imeneyo, chimodzimidzi mwanjira iyo, koma ndimo momwe izo ziliri.

²³⁵ Penyani! Apa mpingo waukulu, woyera wa Orthodox, "Ife tikudziwa Mawu. Ife tiri nawo masukulu. Ife tiri nawo maseminare. Ife tiri nawo anthu athu opukutidwa kwambiri! Bwanji, kwa zaka za mazana ife takhala omvera kwa Yehova. Ife ndife Mpingo. Ife ndife Sanhedrin. Ife tiri ndi Bungwe la Mpingo kuno. Onse Afarisi ndi Asaduki, ndi zipembedzo zonse, zimasonkha pamodzi," monga ife tikuchitira. Mukuwona? "Ife tonse tiri mu chimodzi, b—Bungwe la mpingo. Ife ndife opeza bwino kuno. Ife tikulidziwa Lemba limenelo. Ndi chiyani wina wamng'ono, munthu wosadziwa kumusi uko pa mtsinje, ali ndi ndevu yavi pa nkhope yake, ndi chidutswa cha chikopa chankhosa, kutiwuza ife?" Ndithudi, awa sakanamvera kwa Ichu.

²³⁶ Koma Baibulo linanena, mu Malaki mutu wa 4... kapena mutu wa 3, "Ine ndidzatumamiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, kuti andikonzere Ine njira." Zaka mazana asanu ndi ziwiri ndi khumi ndi ziwiri pasanafike apo, Yohane... O, mneneri wamkulu wa Yesaya anayima pamenepo, ndipo anati, "Padzakhala liwu la mmodzi wofuwula mu chipululu, 'Konzani njira ya Ambuye, ndi kupanga njira Yake ikhale yowongoka.'" Uko nkulondola. Ndipo anati... ndipo Dav-... O, ambiri a iwo! Anati, "Malo onse okwera adzatsitsidwa."

²³⁷ O, iwo anati, "Padzakhala... Pamene munthu uyu abwera, iye adzalozza chala chake, ndipo iye adzasuntha mapiri. O, ndipo malo onse otsika, mayenje, adzakwezedwa. Ndiye onse, ndiwo malo onse okumbika, adzasalazidwa. M'bale, tidzabzala chimanga mu munda uliwonse kuzungulira pano. Ndipo, o, ife tidzachita zinthu zazikulu pamene munthu uyu abwera." Mukuwona?

²³⁸ Iwo anali kuyembekezera Mulungu kuti atenga chipukusiro ndi kuchipukusa icho, kutsitsira khonde pansi, kunena, “Bwerani pansi, inu wotsogolera wamkulu wa Mesiya.” Ndiyeno mwamsanga iye akapita, iwo akukokeranso icho mmwamba, ndipo utumiki wake watha. Iwo achitsitsa icho pansi kachiwiri, ndi kuchisiya icho pansi ponwe apa pambali pa seminare, ndi kunena, “Chabwino, Mwana Wanga wokonedwa, yenda kupita kupita pansi ndipo kawawuze iwo.” Mwawona? O, mai!

²³⁹ Penyani, pamene iye anabwera. Chirichonse chomwe chinachitika? Apa panabwera munthu yemwe sankayidziwa iliyonse ya sukulu zawo. Analibe ngakhale khadi lachiyanjano. O! Analibe zomuvomezetsa. Ayi. Palibe aliyense ankadziwa kuti iye anapitako ku sukulu kwa tsiku mu moyo wake. Inu simukanakhoza ngakhale kudziwa izo mwa kulankhula kwake. Iye sankalankhula ngakhale mwa kulankhula kwa... kwa zazipembedzo. Iye ankalankhula za maserpeni, nkhwangwa, ndi chipululu, ndi—ndi—ndi zinthu monga izo, mwawona, mitengo. Iye sankalankhula mwa kulankhula kwa kakhazikitsidwe ka zazipembedzo za tsiku, kapena za tsiku lino, kapena tsiku lina lirilonse.

²⁴⁰ Iye anabwera “sassafras,” monga ife timatchulira izo kuno mu Indiana. Iye akubwera kuchokera kuthengo kwinakwake. Sanali ngakhale atameta, ndipo tsitsi liri chang’alang’a pa mutu wake. Ine sindikuganiza iye ankasamba; kamodzi pa miyezi iwiri kapena itatu. Kulondola. Iye sankavala zovala zogonera usiku. Iye sankakwera konse mu galimoto. Iye sankapukuta konse mano ake. O, mai! Anali munthu wotani uyu! Ndithudi ayi.

²⁴¹ Apa iye akubwera, akumbambanda kupyola mu chipululu, monga choncho, anati, “Ine ndine liwu la mmodzi wofuula mu chipululu. Konzani njira Ambuye, ndi kuwongola mozera Mwake!”

²⁴² Ena a aziphunzitsi anayima nati, “Ha! Nnena, munthuwe, kodi iwe uli nacho chako... Ife sitingakhoze kuyanjana nawe iwe mu msonkhano uwu. Apa, ife sitingachite ichi. Chabwino, liri kuti lako—liri kuti khadi lako? Chizindikiritso chako chiri kuti?” Iye basi sanawasamale iwo. Iye anali ndi uthenga, kotero iye anangopitirira nawo iwo, inu mukuwona, kulalikirira basi chimodzimodzi.

²⁴³ Iwo anati, “Bwanji, dikirani! Chabwino, ngati ife tipite kumusi uko, ife tikawatengera a bishopu kumusi, lero, ndi kuwona chimene iye ati anene za icho. Ife tipita kumusi uko ngati ife tikudziwa. Amenewo ndi akulu a mpingo. Ndipo ife tikudziwa iye adzayenera kuwazindikira iwo. Ngati iye ali wa Mulungu, iye adzawazindikira mabishopu athu.”

²⁴⁴ Kuwayika iwo onse pamenepo mu mndandanda, ndipo anayima kunja uko, amawudindo.

245 Iye anati, “Inu m’badwo wa amamba! Inu njoka mu udzu!” Makolala otembenuzidwa, ndi “abambo oyera,” ndi zina zotero. “Ndani wakuchenjezani inu kuti muthawe mkwiyo umene uli nkudza? Inu mukudziwa ora lanu liri pafupi. Musati inu muziganiza kuti. . . Inu mukuti, ‘Chabwino, ife tiri a *ichi, icho.*’ Ine ndikukuwuzani inu, Mulungu yemwe ine ndikumtumikira ali wokhodza kuwutsa ana kwa Abrahamu kuchokera mu miyala iyi.” O, mai!

246 Tsopano iye akuwutenga wake mosemphanitsa, kuchokera mu kulankhula kwa zachipembedzo. “Ine ndikuti nkhwangwa yagonekedwa ku muzu wa mtengo! Chotero mtengo uliwonse womwe subala chipatso chabwino ugwetsedwa pansu ndi kuponyedwa mu moto! O, Ine indedi ndikubatzani inu ndi madzi, kwa kulapa, koma Iye ali kubwera pambuyo panga. Mwezi udzasandulika magazi! Ndipo, o, mai, Iye adzayeretsa kwathunthu madwale Ake! Ndipo Iye adzatenga m—mungu ndipo adzawutentha iwo ndi moto wosazimitsika, ndipo Iye adzatengera tirigu ku nkhekwe. Iye adzalekanitsa mawudzu ndi tirigu.” O, mai! Uthenga wotani!

247 Iwo anati, “Munthu ameneyu! Ha! Iye wati chiyani, inali nthawi yanji—yanji—yanji? O, umbuli! Ife tiri naye munthu kumtunda komwe uko, M’bale Jones. Iye ndi munthu yemwe ati adzachite izo, ngati alipo aliyense mu m’badwo uno. Bishopu *Wakuti-ndi-wakuti* adzachita izo; Bambo Woyera *Wakuti-ndi-wakuti.*” O, mai! Mukuwona?

Mulungu mu kuphweka, mwawona, kugwira ntchito mu kuphweka.

248 Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye akuyima pamenepo tsiku lina, ndipo iye anati, “Inde, Iye wayima pakati panu!” Iye anali wotsimikiza kuti iye anali wotsogolera uja. Iye ankadziwa chomwe iye anali. Ndicho chifukwa chake iye ankakhoza kuwachotsa iwo zikopa. Anati, “Tsopano, musati munjenjemere, koma ingomapitirirani ndi kupitirizabe. Inu asirikali, inu muzimvera mabwana anu. Ndipo ngati inu mwachita choyipa chirichonse, inu muchitenge icho. . .”

249 “Ife tidzachita chiyani? Kodi ife tisiye kumachita *izi*? Kodi ife tileke kuchita *izi*?”

250 Iye anati, “Ingomapitirirani monga inu muli. Zipitiriranibe. Zipitiriranibe. Pitani patsogolo. Ngati inu mukulima mbatata, limani izo. Mukuwona? Inu asirikali, musati muchite chosokoneza ayi. Ndipo—ndipo inu muchite *izi*. Ndipo chirichonse chimene inu mukuchita, zipitiriranibe basi monga inu muliri. Amvereni mabwana anu, ndi zina zotero.”

“Mphunzitsi, ife tichite chiyani?”

251 “Zipitiriranibe basi monga inu muliri, mwawona. Koma pali Mmodzi pakati panu, yemwe inu simukumudziwa.” Iye ankadziwa kuti, ora la uthenga wake. Iye amadziwa kuti iye

anali woti akamuwonetsere Munthu ameneyo. Iye anadziwa kuti Iye anali pamene. “Mmodzi pakati panu! Inu simukumuwona Iye. Zinthu zikuchitika, inu simukudziwa kanthu za izo.” Ndipo kotero, ndiye, “Apo—apo pali chinachake chiti chichitike,” iye akuti, “inu mukuwona, ndipo Iye adzakhala pano. Ndipo ine ndidzamudziwa Iye.”

²⁵² Ndipo potsiriza, tsiku limodzi, iye anati, “Tawonani, apo Iye ali! Apo pali Mwanawankhosa wa Mulungu yemwe achotsa tchimo la mdziko!” Anati, “Ndipo nthawi yanga yatha tsopano. Ine ndakuwonetsani inu kwa Iye. Ine ndiyenera kuchepa tsopano. Ine ndiyenera kuchoka powonekera. Iye apitiriza kuchokera apa.”

“Zakachikwi ziyambika, mosachedwa pomwepa, mwawona, ndipo n—nthawi yayandikira.” Ndiye pamene Iye abwera, pamene . . .

²⁵³ Ngakhale Yohane anati, “Iye adzachita, o, Iye adzakungunula zikopa. Iye adzachita—Iye adzalekanitsa tirigu kwa—kwa mungu, ndipo Iye adzaziwotcha izo. Ndipo Iye adzayeretsa bwinobwino madwale Ake, ndipo chokupizira Chake chiri mu dzanja Lake!” Koma Iye anali chiyani? Wamng’ono, kakang’ono . . .

²⁵⁴ Tsopano, iwo anali nazo izo zonse atajambula, “O, amuna! Iye adzakhala ndi nkondo womwe udzakafike mtunda wa mailo imodzi. Iye adzayima kumbuyo cha kuno mu Palestina, kungoyima kumeneko ndipo basi . . . pa umodzi wa mitambo yoyera iyi, ndi kuwatenga Aroma onse awa, monga *chonchi*, ndi kuwaponyera iwo mu gehena. Kumangochitabe monga *choncho*, mwawona, mpaka Iye atawatha iwo ponseponse.” Bwanji, iwo anali nazo izo zokonzedwa kale.

Ndipo pamene iye anali, Mwanawankhosa wamng’ono kubwera akuyenda pakati pawo, wofatsa ndi waulemu, akukankhidwira mbali *iyi* ndi mbali *iyi*.

²⁵⁵ Ngakhale Yohane ananena. Tsopano yang’anani pa Yohane, mneneri; iye anati, “Pitani mukamufunse Iye. Kodi ali kwenikweni Iye Ameneyo?” Wodzichepetsa kwambiri, mpaka mneneri ameneyo anaphonya chimenecho. Anati, “Kodi Iye ndi Ameneyo, kapena ife tifune wina?”

²⁵⁶ Tsopano, Iye sanamupatse iye bukhu kuti iwo ophunzira, mu—mu Mateyu 11. Anabwera ndi kumufunsa Iye, pamene ophunzira a Yohane . . .

Yohane anali mu ndende. Kotero iye anali yense atasokonezeka chotero mpaka iye . . . Ine ndikukhulupirira anali Pember anati, “Diso lake la mphungu linachita nkhungu, kumusi uko,” inu mukuwona. Iye amakhoza . . . Iye—iye anali atabwera kale pansu ku dziko lapansi; iye anali ali mu mlengalenga. Koma pamene uneneri wake unali utatha, iye anabwereranso ku nthaka kachiwiri, mwawona, chifukwa, anamuyika iye mu

ndende, inu mukuwona. Iye analibenso nawo ntchito mapiko akulu awo, kotero iye anangogona pansu pamenepo. Koma iye anawuluka pamwamba kuposa wina wa aliyense wa iwo.

²⁵⁷ Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Mulungu anamugwiritsa iye ntchito. Ndipo Yesu anadziwa, inu mukuwona, chifukwa uyo anali—uyo anali Mulungu mu thupi uko. Mukuwona? Iye anali... Kotero, Iye—Iye ananena pamenepo, Iye anati...

Tsopano, Iye sanamupatse iye konse bukhu la momwe angakhale wamakhalidwe mu ndende; Iye kuti, “Tsopano dikirani miniti. Ine ndilemba nkhani yaying’ono apa, ndipo inu mubwerere nayo ndipo mukamuwuze Yohane momwe ayenera kukhala ndi makhalidwe pamene iye ali mu ndende, chifukwa cha Ine.” Mukuwona.” Mukuwona? Ayi, Iye sananene konse izo.

²⁵⁸ Iye sananene kuti, “Pitani mukamuwuze Yohane kuti iye ayenera kukhala nayo digri ya Ph.D. iye asanatulukeko.” Mukuwona? Ngati iye akanatero, iye bwezi ali ndi ena onse a iwo; iye akanakhala wokana.

Yohane anali wowona mtima ndipo anafunsa funso.

²⁵⁹ Ndipo Iye anati, “Tangodikirani mpaka msonkhano utatha, ndiyeno mupite mukamuwonetse Yohane chimene chinachitika, ndiye iye akadziwa. Ngati inu mukamuwuze iye zimene zikuchitika, ndiye iye akadziwa.” Mukuwona? Mukuwona? “Ingopitani mukamulole iye... Mukamudziwitse iye. Kamuwuzeni iye ali... Iye ali mu ndende ndipo sakanakhoza kukhala kuno. Koma—koma inu munakhala mu msonkhano, ndipo inu mwawona zomwe zachitika. Inu mupite mukamuwuze iye.”

Kotero, ndiye, ophunzira anati, “Zabwino kwambiri, Mbuye.”

²⁶⁰ Ndipo chokwera phiri iwo anapita. Yesu atakhala pa mwala uwu, kumangowayang’ana iwo mpaka iwo atawoloka ndi kupita chokwera phiri.

²⁶¹ Iye anapotolokera kwa osonkhana, anati, “Kodi—kodi inu munapita kukawona ndani, mu nthawi ya Yohane?” Mukuwona? Anati, “Inu munapita kukawona chiyani? Kodi inu munapita kukawona munthu yemwe ali ndi kolala lotembenuzidwa, ndi zovala zofewa, ndi wopukutidwa—mwapamwamba ndi wophunzira. Kodi ndiwo mtundu wa munthu yemwe inu munapita kukamuwona?” Anati, “Ayi. Inu mukudziwa chomwe mtundu umenewo uli? Iwo amapsyopsyona makanda, ndipo, inu mukudziwa, amagwira ntchito mu nyumba zachifumu. Iwo, kuti—sindiwo mtundu umene Yohane anali.”

²⁶² “Chabwino,” anati, “ndiye, chifukwa chiyani inu munapita? Kutu mukawone munthu yemwe wapatsidwa utumiki ndipo adzawulumikiza iwo ku bungwe, kapena chinachake monga

icho? Wogwedezeke nalo lirilonse... Ndiye, ngati a—ngati a Umodzi sakumufuna iye, iye apita ku Utatu? Ndipo ngati a Utatu sakumufuna iye, iye apita ku mpingo wa Mulungu, kulikonse? Kodi ndiwo mtundu wa munthu yemwe inu munapita kukamuwona, wogwedezeke ndi bango lirilonse? O, ayi. Osati Yohane.”

²⁶³ Iye anati, “Ndiye inu munapita kukawona chiyani? Mneneri?” Iye anati, “Ndipo Ine ndikuti uko nkulondola. Koma Ine ndikuwuzani inu chinachake chimene inu simukuchidziwa; iye anali woposa mneneri. Iye anali woposa. Ngati inu mungakhoze kulandira icho, uyu ndi iye yemwe analembedwa, mu Baibulo, mwawona, kumbuyo uko, mu Lemba, ‘Ine ndidzatuma mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga,’ Malaki 3, mwawona, ‘ndipo iye adzakonza njira patsogolo Panga.’” Mukuwona?

²⁶⁴ Ndipo iwo sanamvetse. Ngakhale ophunzira sanamvetse izo, mwawona. Uko nkulondola. O, mai! Kuphweka! Khalani wodzichepetsa, mwawona. Pitani pansi pomwe... Pamene Mulungu alonjeza chinachake chachikulu, mwawona, icho ndi chachikulu mwa kupenya Kwake.

²⁶⁵ Tsopano, ngati inu mukufuna nthawizonse kumakumbukira izi, ine ndikufuna inu kuti... Inu musunge izi mmalingaliro. Ndipo pamene izi zichitika, ndiye inu mukhoza kusintha izo. Inu mupite ndi mukathothole limodzi la maluwa a nthawi yophukira masamba aang’ono awa omwe akubwera chaka chino, kapena mukatenge tsamba wamba la udzu ndipo mukaligwire ilo mu dzanja lanu, ndi kunena, “Ine ndigwira ili tsopano, ndi kuwona kuti chinachake icho, chophweka kwambiri, nchimene chinapanga *ili*. Ndipo ine ndikufuna kuwuwona ubongo, womwe ungakhoze kutumiza chombo ku mwezi, upange tsamba la udzu ili.” Inu mudzakhala nalo ilo nthawizonse. Inu mukhoza kudzakhala otsimikizira pa ilo. Inu nthawizonse mudzakhala nalo ilo. Mukuwona? Tsamba la udzu liri nawo moyo mwa ilo, mwawona. Ndi zophweka kwambiri ndi zonyozeke.

²⁶⁶ Inu mukuwona, ngati munthu ali munthu wamkulu, chabwino, koma ngati iye ali wamkulu mokwanira kuti iye akhoza kukhala wophweka, mwawona. Iye adzamupeza Mulungu. Koma ngati iye sakhala wophweka, iye sadzamuwona Iye konse. Koteru inu muyenera kukhala wophweka. Tsopano ndime... .

195. Mu Chivumbulutso, ndime 5:9, ndi ndani awa akupezeka akuyimba—akuyimba pamene Mwanawankhosa akutenga Bukhu kuchokera m... kuchokera m... akutenga Bukhu? Kodi ali—ali awa oyera okwatulidwa?

²⁶⁷ Ayi. Chivumbulutso 6...5:9, kani. Ayi. Ngati inu muzindikire, awa sali oyera. Iwo anali... Iye anali asanatengebe

zinthu Zake. Mukuwona? Awa sali oyera. Ngati inu mutazindikira, iwo ali akulu ndi Zamoyo, ndipo iwo akuyimba.

²⁶⁸ Tiyeni tiwerenge izo, kotero munthu ameneyo. . . Ndiyeno ine ndiyesa. . . Ine ndiri nawo pafupi theka la dazeni ena apa, ndipo ine ndikuganiza ine ndikhoza kuwatenga iwo mu maminiti pang'ono. Tiyeni tiwone. Chivumbulutso 5:9. Tsopano tiyeni tiwerenge pang'onong'ono pokha tisanati. Kotero, munthuyo, tsopano, ali wowona mtima pa izi, ndipo iwo akufuna kudziwa. Yang'anani.

Ndipo pamene iye anali atatenga—atatenga bukhu, zamoyo zinai ndi akulu anai ndi makumi awiri anagwa pansi pamaso pa Mwanawankhosa, ali nawo mmodzi aliyense wa iwo azeze, . . . mbale za golide zodzaza zofukiza, zomwe ziri mapemphero a oyera.

Ndipo iwo anayimba nyimbo yatsopano, (mwawona, mwawona,) kunena, Inu muli woyenera kutenga bukhu, ndi kulitsegula Ilo, (mwawona,) . . . inu mwatiwombola ife . . .

Ndipo . . . mwatipanga ife ansembe ndi mafumu . . .

²⁶⁹ Ndilo gulu la Kumwamba, osati owomboledwa apa ayi. Chabwino, tsopano.

M'bale Branham, ngati onse a . . .

Tsopano mphindi chabe. [M'bale Branham ayimikira—Mkonzi.] Ine ndikuganiza, chiyani . . . Mundikhululukire ine.

M'bale Branham, ngati—ngati onse aumulungu, (eya), aumulungu adzatengedwe mu Mkwatulo, kodi nanga Eliya ndi . . . ndi Mose adzachokera kuti?

²⁷⁰ Pali chinachake chalakwika. Pali chinachake chalakwika. Ndizo chabe zonse ziri kwa icho. Pali—pali chinachake chomwe chachitika. Mukuwona? Pali chinachake chimene chinalakwika penapake. Eliyense akumverera bwinobwino? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Apo ayi. . . Palibe matenda, kapena palibe kanthu?

[M'bale mwa osonkhana ati, “Werengani ndime ya 9 kachiwiri, mu Chivumbulutso 5.”] Tiyeni tiwone, Chivumbulutso . . . Panali pati pamenepo, m'bale? [“5.”] 5. [“5.”]

O, funso! O, funso ine ndangoyankha kumene. Tsopano tiyeni tiwone. “Inu . . .” Malo oyenera:

Ndipo pamene iye anali ata- . . . bukhu, zamoyo zinai ndi akulu anai ndi makumi awiri anagwa pansi pamaso pa Mwanawankhosa, ali nawo mmodzi aliyense wa iwo azeze, ndi mbale za golide zodzaza ndi zofukiza, zomwe ziri mapemphero a oyera.

Ndipo iwo anayimba nyimbo yatsopano, kunena, Inu muli woyenera kutenga bukhu, ndi kutsegula chisindikizo chake: pakuti inu mwachita... munaphedwa, ndi...

Apa icho chiri! Apa icho chiri! Ine ndinalakwitsa pa icho. Mukuwona?

...inu mwatiwombolera ife kwa Mulungu ndi magazi...a mtundu uliwonse...

²⁷¹ Uko nkulondola. Tsopano, inu mukuganiza chiyani za icho? O, ngati Kukhalapo kwa Mzimu Woyera sikuli pano, nchiyani icho? Iye sakanalola...Mwawona, ine ndinangowerenga gawo loyamba la ndime imeneyo. Mukuwona, iyo ili—iyo ili chabe ndim-...kapena chinachake ndalemba apa, ndipo ine ndimayesera kupyola, ndikuyang’ana pa koloko iyo. Koma inu mukumuwona Iye akundiylimitsa ine pa icho? Ulemerero! Mwawona, ine sindinawerenge konse gawo lina la iyo. Mwawona, ine ndinafika apa, “Ndipo...” Penyani apa, “Ndipo iwo—ndipo iwo anayimba nyimbo yatsopano,” ndipo ine ndinayima, mwawona. Koma, penyani apa, “Nyimbo yomwe iwo anayimba, kunena, ‘Inu mwatiwombola ife kuchokera ku mitundu yonse, lirime, ndi fuko.’” Zedi, ndiwo iwo. Mai! O, mai! O, mai! Mwawona icho? Ndipo, tiri chilankhulire, pali funso lina pansu apa, nalonso.

196. Mungakhoze inu (k-u-l-a-m-u-l-i-...) kulamulira iwo amene akupatsidwa...Chabwino, kulamulira “iwo amene akupatsidwa miinjiro yoyera,” a Chivumbulutso 6:11, ndi “iwo amene anatsuka miinjiro yawo mu Magazi a Mwanawankhosa?”

²⁷² Tsopano tiyeni tiwone, Chivumbulutso 6. Ine sindingangothamanga pa ili, anthunu, monga chonchi apa, mwawona, chifukwa izo zipita...Ine ndiyankha chinachake cholakwika. Tsopano, Iye sanafune—Iye sanafune ine kuti ndichite izo. Ndicho chowonadi, koteru ndithandizeni ine. Mzimu Woyera wa Mulungu ukudziwa kuti icho ndi chowonadi. Mukuwona? Ine basi...Panali chinachake basi... Ine—ine ndinangoyang’ana pa iyo...Ine ndinali kuyang’ana pa koloko, hafu pasiti leveni, ndipo ine ndinaganiza, “Ngati ine sindifulumira tsopano, ine sindifika popempherera odwala.” Ndipo ine ndikuyesera kutenga izo. Chifukwa ine...Ndipo malingaliro anga ali chotero... Ine sindingakhoze...

²⁷³ Inu mukukumbukira, inu mukungoyenera kumvetsa tsopano, ine—ine ndine munthu, mwawona. Ndipo ine—ine ndakhalala ndiri mmenemo kwa masiku asanu ndi awiri, ndi anga... Ndipo ine ndiri nachobe chinachake, madzulo ano, ine ndiyenera kupeza kuchokera kwa Mulungu.

²⁷⁴ Koma, Iye anali wotsimikiza kuti ine sindikanapanga kulakwitsa kuja, iwo anandiyitanira ine mmbuyo kuti

ndiwerengenso ndime yonseyo. Ine basi...Ine basi ndinangomverera ngati Chinachake chikungogudubuzika pa ine pamenepo, ndipo anati, “Bwerera mmbuyo! Bwerera mmbuyo!”

Ine ndinaganiza, “Bwerera mmbuyo”? Chiyani? Yima pakali pano ndipo yamba kupempherera odwala? Koma chiyani—ndi chiyani icho? Ine ndachita chiyani?”

Ndipo basi ine ndinayamba kufikira chimenecho, winawake anati, “Werangani ndimeyo kachiwirinso.” Ndipo ine ndinawerenganso iyo. Ndipo apo, mmusi mwa funso ili, apo icho chinali, mwawona, “Chivumbulutso 6.”

²⁷⁵ Mwawona, ine ndinawerenga yoyamba. Iyo ikumveka ngati iyo, yoyamba, mwawona, “Ndipo iwo anayimba nyimbo yatsopano.”

Koma mmusi muno, mwawona chimene iyo inali? Yotsatira, kubwera mpaka mmusi, “Watiwombola ife.” Zedi, uyo anali Mkwatibwi, oyera okwatulidwa. “Mukanakhoza inu. . .” Ndipo apa, ndithudi, m—Mwanawankhosa anali nalo Bukhu mu dzanja Lake. Iye anali atachoka kale pa Mpando wa chisomo cha ukhalapakati. Mukuwona? Inu mukuwona momwe Mzimu Woyera umayang’anira izo? Chifukwa, chimodzimidzi, ndicho chinthu chomwecho ine ndinanena usiku wina.

²⁷⁶ Pamene Iye anali atalankhula kwa ine mu chipinda, ndipo ine ndinabwera kumusi kuno ndipo ndinalalikira kwa inu nonse, kuti, “Pamene Mwanawankhosa anasiya malo.” O, mai! Tsopano ine ndikukhulupirira ife tingotenga phunziro. Mwawona, “Mwanawankhosa anali atasiya mpando Wake ndi kubwera,” mwawona, pomwe ine ndinafika pamenepo pamene Iye anali alipo, Kuwala kuja, komwe kuli Khristu; pomwe Iye analipo, ndinanena icho. Pamene Mwanawankhosa akusiya pokhala apo pa Mpandowachifumu, pokhala Mkhlapapakati, Iye akubwera apa, ndipo Tsiku la Chiwombolo kwa Mpingo latha.

²⁷⁷ Chiwombolo chotsatira chatsegulidwa, chiri cha kwa Ayuda, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi. Ndi kulondola uko? Chifukwa Iye analonjeza kuti Iye udzawudula mtengowo, inu mukudziwa.

²⁷⁸ Tsopano, apa, tsopano apa Iye akutulukira, Mwanawankhosa, ndiyeno Tsiku la Chiwombolo latha. Ndipo onse amene ati awomboledwe, awomboledwa kale ndipo ayikidwa pa Bukhu, ndipo Iye ali kunja kuno akutsegula Bukhu. Kulondola!

²⁷⁹ O, tikukuthokozani Inu, Ambuye. Mukuwona? Khululukirani wantchito Wanu wamanjenje poyesa kuthamanga kudutsa chinachake.

Tsopano, kodi inu mungakhoze kulekerera “iwo akupatsidwa miinjira yoyera,” a Chivumbulutso 6:11. . .

²⁸⁰ Tsopano tiyeni tiwone, 6:11. Chabwino. Ife tiri pati tsopano pa ili? “Miinjiro yoyera,” eya, ndiwo—wopachikidwa, pansu pa guwa. A—Ayuda, pakati pa nthawi imeneyo, “Two anapatsidwa miinjiro yoyera.”

. . . ndi “iwo omwe anatsuka miinjiro yawo mu Magazi a Mwanawankhosa,” a Chivumbulutso 7:14?

²⁸¹ Ayi. Tsopano, izo ndi zosiyana, kutsimikiza mokwanira. Chifukwa, mwawona, apa, ife tikupeza *apa*, kuti “awa anapatsidwa miinjiro yoyera,” cha apa mu nthawi iyi. “Iwo anapatsidwa miinjiro yoyera,” iwoeni, mwa chisomo. Ndipo awa *apa*, “Anali atatsuka miinjiro yawo mu Magazi a Mwanawankhosa,” ndipo cha mu Chivumbulutso cha apa, awa ndiwo “khamu lalikulu lomwe linabwera pamaso pa Mulungu, a mitundu yonse, malirime, ndi mafuko.” Ndipo *awa* ali molunjika chimodzimodzi kwa ofera, Ayuda, inu mukuwona. Tsopano, tsopano izo ndi zolondola, tsopano.

197. M’bale Branham, ngati onse aumulungu anatengedwera mmwamba mu Mkwatulo, Eliya ndi Mose adzakhokera kuti? Kodi iwo adzakhala Ayuda? Kapena adzakhala Eliya wathu, yemwe waperekedwa kwa ife, kukhala—akakhala ndi iwo?

²⁸² Ayi. Wa—Wamitundu yemwe adzadzozedwe nawo mzimu uwu, kuti akawatulutse Amitundu, adzakhala atachotsedwa. Chifukwa, inu mukuwona, Mpingo wonse, onse, atengedwera mmwamba. Ndipo aneneri awiri awa, a—a mutu wa 11, akubweretsedwa pansu. Ndipo tsiku la chisomo lathana naye Wamitundu, ndipo chatumizidwa kwa Ayuda. Ayi, uyo sadzakhala munthu yemweyo. Tsopano, ine ndiri—ine ndiri wotsimikiza ndithudi za izo. Tsopano kumbukirani, izi ziri chabe mwakukhoza kwa kudziwa kwanga.

Tiyeni tiwone chomwe ili liri, likunena apa. Funso, “Ali tirigu ndi vinyo. . .” O, “Ali. . .” T-i-r-i-g-u. Ayi, ine ndikuganiza ilo—ilo limatanthawuza, “Ali chiyani. . .” Ilo liribe “kodi” pamene. Likungonena:

198. Ali chiyani ndi vinyo, kapena tirigu ndi vinyo, ali chiyani a . . . wa Chivumbulutso 6:6?

Tiyeni tiwone chomwe ilo liri, pamene ine ndifika mmusi apa tsopano, izi apa.

Ndipo ine ndinamva liwu mkati mwa zamoyo zinai likunena, Muyeso wa tirigu wogula rupiya, ndi muyeso wa barele wogula rupiya; . . . penya kuti iwe usawononge vinyo ndi. . . mafuta.

²⁸³ Ine ndikuganiza ndiko kutanthawuza “tirigu ndi vinyo.” Izo zinali chimodzi, kwa chimzake.

Kani, kodi ndi chiphiphiritso, vinyo womwedwa pa gome la mgonero, wa Chivumbu- . . . wa Akorinto Woyamba 11:24?

284 “Kodi vinyo—vinyo...” Ayi. Chimodzi cha izo ndi chophiphiritsa chawuzimu, mwawona. Ndipo chimodzi chinacho chiri makamaka v—vumbulutso la Mawu.

199. Kodi zingakhoze kukhala chifukwa chomwe ambiri akudwala, chifukwa ife sitinalizindikire Thupi la Ambuye? (Kukhoza!)

...koma tsopano zawululidwa pa kutseguka kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi?

285 Tsopano, tiyeni tiwone. Ndiroleni ine ndingowona ngati ine ndingakhoze kutenga izo tsopano. Si inu; ndi ine. Inu simunati . . . Inu munalemba izo zonse molondola; ndi ine basi.

Kodi zingakhoze kukhala chifukwa chake ambiri akudwala, chifukwa ife sitimalizindikira Thupi la Ambuye? (Ilo liri ndi chizindikiro cha funso, kumapeto a ilo.)

286 Chabwino, Lemba likunena, kuti, “Ambiri ali odwala ndi ofowoka pakati panu, chifukwa cha kulizindikira kwa Thupi la Ambuye.” Ndizo chimodzimidzi zolondola. Chifukwa, mwawona, Thupi la Ambuye ndi Mkwatibwi. Ndipo ambiri a iwo amapita kumbali, ndipo iwo samapita nalo Ilo. Izo nzowona. Mwawona, iwo samadziwa momwe angamakhalire iwoeni khalidwe. Amakhala moyo wa mtundu uliwonse; ndi kumatenga mgonero ndi zinthu. Izo sizolondola. Mukuwona? Pamene anthu atenga mgonero, omwe amanama ndi kuba ndi kumwa, ndi, izo—izo—ndizo zoyipa. Inu musamachite zimenezo. Mukuwona?

...koma tsopano zawululidwa mwa kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi?

287 “Kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi.” Tiyeni tiwone tsopano. Ayi. Tsopano, inu mupeza kuti, Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi chikutseguka apa, chinali kwa Ayuda. Mukuwona, m—Mpingo wapita kale. Iyi ndi nthawi ya Chisawutso, kotero izo sizikanakhala zofanana. Ayi. Ayi. Izo siziri.

288 Chimodzi cha izo chiri vinyo wauzimu, ndilo vumbulutso la Mawu, ndiye—wokhulupirira amakhala wokondowedwa ndi vumbulutso la Mawu. Ndipo chinacho chiri chophiphiritsa cha Magazi a Yesu, omwe amatengedwa pa gome la Ambuye. Tsopano, ndiko kukhoza kwa kumvetsa kwanga kwa izo.

200. Kodi aliyense yemwe sanakonzedweretu adzalandira Ambuye? Ngati iwo atero, kodi iwo adzagwa?

Osati ngati iwo ali okonzedweratu. Ayi. Mwawona, iwo sangakhoze.

201. Liri kuti Lemba lomwe limasonyeza kuti...kuti Chikatolika chidzanyenga Ayuda ndi kutenga chuma chawo?

²⁸⁹ Tsopano, “Ndi pati chabe pamene ilo limanena kuti—kuti—kuti chiroambo chidzanyengerera chuma?” Ilo silimanena choncho. Koma ife tikulingalira kuti izo zinali. . . Tsopano, usiku wina, inu mukukumbikira. Inu mukayang’ane kwa tepi mwatcheru kwenikweni. Ine sindinanene kuti ndicho chomwe iwo adzachte. Ine ndinati. . . Mwawona, Akatolika ali gulu lolemera kwambiri mu dziko. Palibe wina wonga iwo. Ndipo chomwe iwo alibe, Ayuda ali nazo zinazo.

²⁹⁰ Ndiko komwe chuma cha dziko lino tsopano. . . Ife tiri pakali pano kukhala moyo pa ndalama za msonkho, molingana ndi *Lifeline*, izo zochokera ku misonkho (zomwe zimabwera kumene kuchokera ku Washington, D.C.) zomwe ziti zidzalipiridwe mu zaka makumi anai kuchokera lero. Ndizo zomwe ife tikugwiritsa ntchito tsopano. Ndiko kusalika kwake ife tabwererera mmbuyo, kupereka mapepala a ndalama, mwawona, pa misonkho yomwe idzalipiridwe mu zaka makumi anai kuchokera tsopano. Fuko lashota. Ilo lapita.

²⁹¹ Tsopano, Castro, chinthu chokhacho chanzeru chimene iye anachitapo, chinali pamene iye anakopera mphamvu ya ndalama ndi kulipirira ndalama za mapepala, mabondi, ndi kuwatentha iwo, ndi—ndi kusintha ndalama za mapepala. Ndicho chinthu chokhacho iye akanakhoza kuchita.

Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chatsalira kwa United States kuti achite. Tsopano kumbukirani, uyu ndi William Branham, mwawona, akulankhula. Ili ndi lingaliro langa. Kuli kulingalira chabe, kuyang’ana chabe pa izo mu kuyima kwachibadwa, zomwe zikhoza kukhala mwina mailosi miliyoni kumbali. Ine ndikukhulupirira kuti komweko uko, mu ndalama zimenezo. . . “Chikondi cha ndalama chiri muzu wa choyipa chonse.” Ndipo ine ndikukhulupirira kuti motsatira kumene mmenemo mudzayamba kugudubuzika kwa mpira.

²⁹² Tsopano, mpingo wa Chikatolika kumbuyo uko, kuchokera ku kulipirisa misa, ndi zina zotero, ukugwirizira chuma cha mdziko. Inu mukukumbukira, Baibulo linati, “Iye anali wolemera,” ndipo momwe iye analiri. Ndipo, kumbukirani, osati kokha fuko limodzi. Iye ali wolemera pa fuko lirilonse liripo pansu pa Kumwamba. Iye amafikako. Iye ali nazo ndalama. Tsopano, zomwe iwo alibe, Wall Street ali nazo, yemwe amalambulidwa ndi Ayuda.

²⁹³ Tsopano, ndipo inu mukukumbukira, iye anapeza ndalama pamene Yakobo anabwerera (usiku watha ife tinazipeza) ndi kukhala Israeli. Iye kwenikweni anali nazo ndalama. Koma ndalama zake sizikanamugulira iye kanthu, mwawona, kwa Esau. Esau anali nazo, nayenso. Mwawona, onse otsutsa, ndi—ndipo mmodzi. . . Mwawona, ziri chabe monga mwangwiro.

²⁹⁴ Tsopano yang’anani apa. Ine ndinati iwo akhoza kufuna kugwirizana pamodzi pa ndalama, ndipo n—ndipo mphamvu

ya Chiroma kutenga mphamvu ya Chiyuda, ndi ya ndalama, kuswa pangano. Izo zikhoza kusakhala choncho. Mwawona, ine ndikudziwa kuti iwo adzaliswa ilo, koma ine—ine sindikudziwa chifukwa chake, chifukwa icho sichinawululidwe kwa ine za chomwe iwo ati adzachte.

²⁹⁵ Koma penyani. Tsopano, ngati lero, tsopano bwanji ngati lero, chinthu chokhacho chomwe ife tingakhoze kuchita, chingakhale kuchita? Ngati ife tikutenga misonkho (ngati mawu awo ali olondola) kuchokera ku ndalama ya mapepala, kuchokera ku ndalama za msonkho wa zaka makumi anai kuchokera tsopano, inu mukuwona, golide wathu ali. . . Ife tamutsiriza kale iye. Ife tashota. Ife tiribe ndalama iliyonse. Ndipo ife tikukhalira chabe moyo pa kutchuka kwa kale.

²⁹⁶ Ndicho chimene mpingo ukuchita lero, mpingo; osati Mkwatibwi. Mpingo ukukhala moyo pa kutchuka kwa kale komwe iwo unali nako kutsidya pansu pa utumiki wa nthawi ya mkango. “Ife ndife Mpingo! Ife ndife mayi wa Mpingo! Ife tinayamba. . .” Uko nkulondola. Mukuwona? Ndiko kukhala moyo pa mbiri!

²⁹⁷ Amethodisti ali kukhala moyo pa mbiri yawo. Abaptisti akukhala moyo pa mbiri yawo. Ndipo Pentekoste ili kukhala moyo pa yawo. “Ulemerero kwa Mulungu! Nthawi yayitali kale, pamene oyera ankavina mu Mzimu, ndi momwe iwo. . . . Ambuyee anachita *ichi* ndi *icho*.” Icho, ndicho chinachake cha mmbuyo. “Ife tonse takula tsopano, m’bale.” O, mai! Mukuwona? Zonse mbiri ya kale!

²⁹⁸ Fuko lino likukhala moyo—likukhala moyo pa mbiri yakale ya chomwe makolo akale anali, mwawona, ndipo ndicho chifukwa chake ife timaganiza kuti ife tidzapulumutsidwa. Mulungu sanalemekeze Israeli pa zomwe iwo anali, zomwe iwo anali; zomwe iwo anali pamenepo! Zindikirani.

²⁹⁹ Koma, tsopano, apa pali zomwe ine ndikuganiza, zomwe ine—ine ndikuganiza kuti zidzachitika. Tsopano, izo zikhoza kusakhala choncho. Ine ndikukhulupirira kuti nthawi idzafika pamene ife tidzawumirizidwe kupanga nkhaniyo. Ndipo pamene iyo idzakhale, kuti, mmalo mwa ife kumasinthu ndalama ya mapepala. . . . Chimenecho chikanadzachita chiyani kwa Philip Morris? Chimenecho chikanadzachita chiyani kwa—makampani a mowa? Chimenecho chikanadzachita chiyani kwa kampani yopanga zitsulo? Chimenecho chikanadzachita chiyani kwa malonda onse? Chimenecho chikanadzachita chiyani? Icho chikanadzawaswa iwo. Iwo akanadzashota. Koma, ngati, “Ife tingakhoze kungongola ndalama zimenezo.” Inu mukuwona momwe iye aliri wochenjera?

³⁰⁰ Ndiye fuko likudzigulitsa kwa mpingo. Ndiyeno mpingo ndi dziko zalumikizana kachiwiri, ndipo apo iye akubwera.

Mukuwona? Ndi zimenezo. Zindikirani. Chabwino. Tsopano, mu ili:

202. Ngati mmodzi ali mu chiyanjano cha bungwe mwa boma lathu, ndipo akhoza kulankhula zofuna za mtima wake womwe, kapena mu Chowonadi cha tsiku lotsiriza, kodi iye adzatengedwa monga mmodzi wa “mahule”?

³⁰¹ Tiyeni tiwone. “Ngati mmodzi ali mu chiyanjano cha bungwe ali. . .” Chabwino, mwawona, chiyanjano cha bungwe; b—bungwe, limapatsidwa mphamvu ndi boma, kuti lizilankhula. Mwawona, izo ziribe chirichonse chochita ndi mtima wake. Mukuwona? Tsopano, ngati iye ali wokhulupirira weniweni, ndi wobadwa mwa Mzimu wa Mulungu, nthawiyina kapena imzake iye adzatsutsidwa. Mukuwona? Icho sichingakhale chomveka kwambiri ndiyeno iye nkusachiwona icho.

³⁰² Tsopano, ine ndikufuna inu. . .Mwawona, inu mukufuna kukumbikira izi, mzanga, kuti Mulungu—Mulungu samachita konse izo, kapena kuti anachitapo pa nthawi iliyonse, monga ine ndingakhoze kukumbukira, mwawona, koma chiyani. . .

³⁰³ Penyani, Yesu anali c—chiyambi cha zonse izi, chifukwa Iye anali Mulungu, Emmanuele, atapangidwa thupi. Tsopano, penyani pa ichi—Munthu uyu, Yesu. Pamene. . .Kodi inu mumadziwa, pamene Iye anabwera pa dziko lapansi, apo panalibe, ine ndikuganiza, limodzi pa khumi la dziko linadziwa kuti Iye anali pano?

Kodi inu mukudziwa, pamene wotsogolera kudzayo abwera, pamene “mapiri onse,” ndi zinthu ziti zidzachitike, apo panalibe mmodzi pa zana la chiwerengero cha Israeli, ine ndikuganiza, anadziwa konse izo? Kodi sizachirendo izo?

³⁰⁴ Bwanji, uko kunali Ayuda ndi zinthu, ndi anthuponseponse mdziko. Tsopano, kumbukirani, Yesu anabwera kuti akhale mboni, monga Mpulumutsi wa mdziko. Nkulondola uko? Bwanji, uko kunali chabe anthu, pambuyo pa anthu, pambuyo pa anthu, pambuyo pa mitundu, pambuyo pa anthu, omwe sanadziwe ngakhale konse kanthu za izo. Ankapitirirabe, monga ngati dziko silinkadziwa kanthu za izo; koma, nthawi yonseyo, izo zinali kuchitika mu dziko. Mukuwona?

³⁰⁵ Bwanji Iye sanawalole iwo kuti adziwe? Iye anabwera, ndipo awo omwe anali okonzedweratu ku Moyo Wamuyaya anali iwo omwe anamulandira Iye. Sichikanakhala chabwino kunena chirichonse kwa onse a iwo, chifukwa Iye sakanakhoza kuwawombola iwo, chifukwa iwo sanali ngakhale okhoza kuwomboledwa. Chifukwa chiyani izo zinali, pamene ansembe amenewo anayima pamenepo? Pamene, Iye anayenera kubwera ku malo amenewo chifukwa okonzedweratu anayikidwa mmenemo, konsekonse, kotero Iye anayenera kulalikirira kwa iwo monga gulu.

306 Ndipo masikolala otchuka omwe akanayenera kumudziwa Iye, anati, “Munthu uyu ndi Bezezebule. Ife sitilola Munthu uyu alamulire pa ife, ndi zina zotero, mwawona. Ife sitidzachita izo.”

Koma hule laling’ono lakale, ndi Moyo mwa iye, wokonzedweratu ku Moyo Wamuyaya, ndipo dzina lake ndi la chisavundi mu Mawu a Mulungu apa. Anayenda kupita pamenepo, ndipo, nthawi yoyamba Kuwala uko kunakantha kambewu kakang’onoko, mwamsanga iye anadziwa izo. [M’bale Branham anakhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.]

307 Penyani, nsodzi wachikulire anabwera cha pamenepo. Apa Iye anayima pamenepo, akuchita zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi—ndi kumawawuza anthu osiyana zinsinsi za mitima yawo, ndi kumadziwulula Yekha.

Ndipo, mai, apo panali Afarisi atayimirira pamenepo, ndipo anati, “Munthu uyu ndi Bezezebule.” Iwo anali woti akayankhe kwa osonkhana awo.

308 Onse a iwo atayima pozungulira, “Dr. Jones, kodi inu mupita kumusi ndi kukamumvera Munthu uyu? Iye—Iye akuwoneka ngati Iye akudziwa zomwe Iye akulankhula. Iye sakulankhula monga anthu wamba.”

309 “Ine ndikamumvera Iye.” Anapita kumusi uko, mwawona. Eya, Mulungu—Mulungu sakanakhoza konse kufika kwa iye.

Ndipo apo Iye anayima kumusi uko, ndipo Iye anati . . .

Iwo anati, “Tsopano penyani apo. Penyani apo. Apo pakubwera munthu apo. Apo pali mmodzi wa ophunzira Ake. Apo pakubwera munthu tsopano. Tsopano, dzina la munthu ameneyo, ndilo Andreyo. Inu mukukumbukira. O, inu mukukumbukira wachikulire—asodzi achikulire kumusi kuno? Ndiwo amenewo. Eya, apo—apo pali Simoni, m’bale wake. Mukuwona? Ndipo ndiwo—ndiwo ana a Yonasi wokalamba. Tsopano apo iwo . . . Penyani, iye—iye akubweretsa winawake kwa Iye. Ndi ndani uyo? Eya, onani chimene Iye ati achite tsopano. Iye—iye ndi wotsatira pamenepo.” Ndipo iye akubwera kuno.

Ndipo Iye anati, “Dzina lako ndiwe Simoni, ndipo iwe ndiwe mwana wa Yonasi.”

310 “Munthu uyu ndi Bezezebule! Mwawona, Iye ali nawo mzimu wa mtundu wina pa Iye. Iye ndi Munthu wosamvetseka. Mukuwona? Molunjikabe, musati inu nonse mumvetere kwa zinthu monga izo, mwawona. Khalani kutali ndi kumeneko. Ine sindidzapitakonso kwa iliyonse ya misonkhano iyi, komwe, mwawona. Basi chinthu ichi chikatha, ife titulukamo muno. Ife sitidzafika, pafupi chonchi kachiwiri.” Mukuwona? Chifukwa? Tsopano, ndicho chomwe iye anaganiza, ndipo komabe amayenera kukhala iyeyo. Penyani, iwo amene omwe Iye anawadzera anali iwo amene anamupachika Iye. Mukuwona?

311 Koma apo panali kahule kakang'ono komwe aliyense anali atakakankha! Ine sindikuvomereza uhule. Ayi, indedi! Koma ine chabe ndikungokuwonetsani inu Mbewu yokonzedweratu.

312 Penyani pa munthu uyu apa, nsodzi wachikulire uyu, sakanakhoza iye...Baibulo linati iye anali wosaphunzira. Nkulondola uko? Si chokhacho ayi, koma iwe anali mbuli. Tsopano, nkulondola uko kapena kulakwitsa? O, ngati ife tikanakhoza chabe kukhala mbuli kwa zinthu zambiri izi zomwe ife tikuganiza kuti ife tikuzidziwa. Mukuwona? Chabwino. Mwawona, iye anali zonse mbuli ndi wosaphunzira. Ndiyeno iye anayenda kupita kumeneko mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, ndipo Iye anamuwuzwa iye yemwe iye anali. Pomwepo icho chinakhazikitsa izo.

313 Tsopano, chotsutsa cha munthu wina uyu ndi chiyani motsutsa icho? “Chabwino, penyani, iye anakhulupirira icho. Penyani yemwe iye ali. Inu mukudziwa yemwe uyo ali. Chabwino, munthu ameneyo sanali...Bwanji—bwanji, iye ndi nsodzi. Bwanji, iye sadziwa ABC wake. Ine ndinagula nsomba kwa iye; iye samakhoza ngakhale kundilemba ine risiti. Uyo, mwawona, ndiwo mtundu wa zinthu! Ndiwo mtundu wa anthu womwe umamvera kwa zinthu monga Izo.” Tikuthokoza Ambuye. Ameni. Mukuwona? “Bwanji—bwanji, iye sakuti... Penyani pa abambo ake; iwo anali osaphunzira. Iwo sanawatumize nkomwe iwo ku sukulu.” Koma ndiwo iwo omwe Iye anawatumiza ku sukulu; anawaphunzitsa mwanjira yomwe Iye amafunira.

314 Ine sindikulimbikitsa kusapita ku sukulu, tsopano. Ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa. Koma apo pali chabe choyimira, mwawona, chomwe inu muti mupeze mmenemo. Ndiwo mtundu, ndi chifukwa chomwe izo zimadutsira pamwamba pa iwo.

315 Ndipo inu mukudziwa chiyani? Osati mmodzi...Ine ndikanati, mwina osati mmodzi pa atatu a Ayuda onse mu dziko anadziwapo kalikonse za Iye kubwera. Ndipo—ndipo, ndiye, mmodzi—mmodzi pa asanu wa mmodzi pa atatu anamvera kwa Iye. Ndipo, ndiye, mmodzi pa zana wa mmodzi pa asanu anawalandira Iwo. Inu mukudziwa kuchuluka kwa omwe Iye anali nawo. Iye anali nawo khumi ndi awiri atayima pa mtanda, kuchokera mu gulu lonselo. Ali kuti onse a iwo? Mukuwona? Makumi asanu ndi awiri anachoka.

316 Tsopano, pamene Iye anali kuchiritsa odwala, ndi kumangopita mmusi, osanena kanthu za Chiphunzitso Chake; Iye ankangopitirira basi, kuchiritsa odwala ndi chirichonse. O, mai! Uwo, uwo unali Mzimu wa Mulungu pa Iye. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Pamene Iye anali kuchiritsa odwala, zodabwitsa! “Ameneyo ndi Mphunzitsi wamkulu. Nnena, abale inu nonse, inu nonse

mukuyenera kukhala naye Iye mu mpingo wanu. Mnyamata, inu mukakamba za mphamvu, Munthu uyo akhoza kwenikweni kuchiritisa odwala! Inu muyenera kuwona. Iye ali nayo mphatso ya machiritso.”

³¹⁷ Chabwino, ndithudi, iwo akhala nazo zokopera zina kwa iyo. Apa iwo akubwera motsatira, chifukwa gulu lililonse liyenera kukhala nalo munthu wawo wawo.

Apa Iye akubwera. Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, tsiku limodzi Iye anakhala pansi.

“O, zedi, Mphunzitsi, ife tiziyenda nanu Inu.”

³¹⁸ “Chabwino, khalani pansi. Tiyeni tizipita.” Chabwino, anawatumiza makumi asanu ndi awiri, ndi zina zotero.

Ndiye tsiku limodzi, kutatha kuchitika kwa chozizwitsa chachikulu, Iye anakhala pansi ndi kuyamba kuwawuza iwo Mawu, mwawona. “Pa kuyamba kwa kuwomba kwa...” Chabwino. Iye anayamba kuwawuza iwo Mawu, Chowonadi.

Iwo anati, “A, tsopano, dikirani kaye! Ha! Ine sindikudziwa za *Ichi*.” Icho ndi chosiyana kwa chiphunzitso chawo. Akuti, “Chabwino, ine ndikudziwa ife tinasiya sunagoge ndi chirichonse monga choncho, koma mwinamwake ife—ife tinalakwitsa, abale. Ife kuli bwino tibwerere, chifukwa Munthu ameneyo akulankhula mu zining’a. Iye ali ngati Munthu wosamvetseka. Ine sindingakhoze kumvetsa *Izo*.” Mukuwona? Chinali chiyani icho? Mbewuyo siyinali yokonzedweratu kuchokera koyamba.

³¹⁹ Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, Iye anali nalo gulu laling’ono la azitumiki, ndipo analankhula kwa atumiki. Iwo anati, “A! Hum! Kuli bwino ife tibwerere, nafenso, ndi kubwerera ndi kukakhala mu bungwe, kutenga zikalata zathu kachiwiri, mwawona. Chifukwa, Munthu uyu, bwanji, ndani angakhoze kumumvetsa Munthu wonga uyo? Iye akunena *ichi* apa, Ndipo akunena *ichi* apa kuno. Ha!”

³²⁰ Iwo enawo sanazimvetse Izo monga choncho. Iye anali kuwasonyeza zining’a kwa ena a iwo, koma osati kwa enawo.

Kotero iwo anachokako. Ndiye Iye anapotoloka pozungulira ndi kuyang’ana kwa khumi ndi awiri atayima pamenepo. Anati, “Inu mukufuna kupita, inunso?” Mukuwona?

³²¹ Tsopano yang’anani. Petro anati, “Inu mukudziwa chiyani? Ine ndinkapitako ku malo akale aja kumusi uko nthawi yonse ija. Ndi kuti mu dziko komwe ine ndingapite? Ndingapite kuti ine? Ndi kuti—nkuti ine ndingapite? Nditatha kuchita kuno ntchito. . . Ndipo ine sindingakhoze kubwerera ku chidebe cha zonyansa icho kachiwiri, komwe uve wonse wa mdziko ukugona mmenemo. Mukuwona? Ine—ine. . . Nkuti komwe ine ndingapite? Ine—ine sindingakhoze chabe kuchita izo.”

³²² Iye ananena, “Ndiye, chabwino, zibwerani, zitsatirani.” Tsopano, apo inu muli. Mukuwona? Izo zinali motani, ndiye? Khumi ndi awiri kuchokera mu pafupi mamiliyoni awiri ndi theka. Ndipo Mpulumutsi wa dziko, kuchokera mu mabiliyoni, komabe wodzichepetsa, mukuwona. Ingokhalani odzichepetsa. Yang’anani.

Tsopano, ndi Afarisi onsewo; ndipo kahule kakang’ono kaja kanabwera kumeneko. Iye anati, “Nnena, Inu muyenera kukhala mneneri! Tsopano, ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, ndipo pamene Iye abwera Iye adzachita zimenezo.”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

³²³ Iye anati, “Ndi zomwezo,” ndipo kutali iye anapita. Inu muyesere kumuyimitsa iye kamodzi? Inu simukanakhoza kuchita izo.

203. M’bale Branham, moni mu Dzina la Ambuye Yesu. Chonde fotokozani yemwe munthu, mu Mateyu 22:11, munthu yemwe sanavale chovala chawukwati, sanavale chovala chawukwati. Ine ndikudziwa munthu uyu akhoza—sakanakhoza kufika Kumwamba wopanda kuvala chovala chachikwati. Uyu anali mlendo, ine ndikudziwa, osati Mkwatibwi.

³²⁴ Inde, uko nkulondola. Iye akanakhala...Eya, iye anangozembera mkati. Mukuwona? Tsopani penyani. Tsopano, ine... Izo zikhoza kutenga ulaliki wonse pa izo.

Tsopano ine ndiri ndi maminiti khumi, kuti ndipempherere odwala ndi kutsiriza awa apa. Ndipo ine ndatsiriza theka limodzi la iwo, ine ndikuganiza. Zindikirani. Koma ine ndiri—ine ndifulumira, kulondola, motsimikiza ndithu, likatha limodzi ili. Mukuwona?

³²⁵ Apa pali zomwe zinachitika, ngati inu mukuyidziwa miyambo yachikale. Mukuwona? Pamene mkwati apereka zoyitanira ku chikwati chake, iye amangopereka kuyitanira kochuluka. Ndipo kwa choyitanira chirichonse iye anatumiza, iye amakhala naye wapakhomo atayima pa khomo, kuti amuveke iye mwinjiro. Kaya iye anali wasawuka, kapena chirichonse iye anali, iye anali...ngati iye anali wolemera kapena wasawuka, chirichonse chomwe icho chinali, iye, onse, anali woti avale chovala cha ukwati ichi.

³²⁶ Pamene iwo anayima pakhomo, iwo ankaveka uwu pa iye, iwo unkaphimba chomwe chakunja chake chinali. Iye wayitanidwa, kaya iye ali wa ndalama mamilioni kapena iye ali wasawuka kwambiri, kapena iye ali mchikumbe, wokumba dzenje, kapena chirichonse chimene iye ali, kapena munthu wolemera, iye ali—iye ali apa atavala mwinjiro tsopano. Chifukwa, mwinjiro unkaavedwa pa iye pa khomo, pamene iye akulowa mkati pakhomo.

